Uvangeri Wa M'nthawi Yotsiriza



Zikomo inu, M'bale Orman.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu kwa mphindi chabe tsopano kwa mawu a pemphero. Ndipo pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ine ndikudabwa ngati alipo aliyense pano amene angakhale ndi chopempha chapadera angafune kuti chidziwike ndi dzanja lokwezedwa? Ambuye amawona zinthu izi, ine ndikutsimikiza. Ndikudalira kuti Iye apereka izo.

2 Atate athu Akumwamba, ife tasonkhana mmawa uno osati kwa cholinga china kuposa kudzakweza Dzina la Ambuye wathu Yesu. Ndipo ife tikukuthokozani Inu kuti ife tamverera kale Kukhalapo Kwake. Ndipo ife ndi otsimikiza kuti Iye akomana nafe, chifukwa ilo ndi lonjezo Lake, kuti "Paliponse pamene awiri kapena ochulukirapo adzasonkhana pamodzi mu Dzina Langa, Ine ndidzakhala pakati pawo." Tsopano, ife tikupempha madalitso Anu, Ambuye, pa zopempha zonsezi lero zomwe zadziwika tsopano pokweza manja mmwamba. Inu mukudziwa chimene chinali pansi pa dzanja limenelo, mu mtima, ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mumuyankhe wina aliyense.

3 Ife tikukuthokozani Inu lero chifukwa cha mwayi wodzakupembedzani Inu. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha mpingo ndi anthu ndi abale a Chikhulupiriro chofanana chofunikira. Ndipo tsopano ife tikupempha kuti Inu mupereke kwa ife zokhumba za mtima wathu lero, zomwe ziripo, kuti tizikutumikirani Inu. Tidyetseni ife ndi Manna obisika amenewo amene Inu munati, mu Baibulo, ankaperekedwa, amene ankaikidwa kumbuyo a unsembe wokha. Ndipo ife timaphunzitsidwa kuti ndife ansembe a Mulungu, tikupereka nsembe yauzimu, ndizo, zipatso za milomo yathu, kumapereka matamando kwa Dzina Lake. Tsopano, ife tikupemphera kuti Inu mutidalitse ife mu gawo lopitirira la msonkhano uno, kunyemera Mkate wa Moyo kwa ife. Mu Dzina la Yesu. Ameni.

4 Ndine wokondwa kuwona banja lathu lalikulu litabweranso kachiwiri mmawa uno, ndipo ndine wokondwa kudzakhala pano ndi inu. Ndipo, komanso, alendo amene akuyenda m'madera osiyanasiyana a dzikoli, amene anasonkhana ndi ife Lamlungu mmawa, ali pano. Ife tiribe chipembedzo. Ndipo ife timangosonkhana, anthu amene amakhulupirira mwa Mulungu amasonkhana pamodzi kuti tidzawapembedze Ambuye pamodzi, ndi kupereka mapemphero athu kwa Mulungu, kupanga kuvomereza kwathu kwa Iye. Ndipo Lamlungu

lirilonse ndi tsiku lirilonse ife timadutsa mu purigatorio, ndiko kuti, kutsuka miyoyo yathu ndi Mzimu Wake Woyera, kuchokera ku machimo athu, kuyesetsa kumakhala moyo waumulungu monga ife tikudziwira mu m'badwo uno wa pakali pano, kumayembekezera kuwonekera Kwake nthawi iliyonse. Ndipo ife tikuyembekezera zimenezo nthawi iliyonse.

5 Tsopano, ife tiri ndi—dongosolo lalikulu lero. Ife tiri ndi misonkhano yathu ya Sande sukulu pano mmawa uno, ndipo kenako usikuuno ife tikhala ndi—dongosolo lapadera kwambiri usikuuno. Mzanga wabwino, M'bale Joseph Boze, amene, iye si mlendo kuno ndi ife, koma ine ndikukhulupirira kuti ndi pafupifupi nthawi yoyamba imene iye anayamba watichezerapo ife mu tchalitchi. Ndi. . .Ine nthawi zonse ndinali ndi mipingo iwiri ya dziko lonse lapansi lomwe ndimayendako, yomwe ndimaitcha nthawizonse "mipingo yachitsanzo," ndipo umodzi wa iyo unali wa M'bale Joseph Boze, Philadelphian Church mu Chicago, Illinois, ndipo winawo unali wa M'bale Jack Moore, Shreveport, Louisiana. Ine ndinkakhala ku mipingo imeneyo mochuluka kwambiri mpaka kuti pamene ndikubwera kwathu kuchokera ku maulendo a umishonare winawake anati, "Musamaimbire ku Jeffersonville kuti mumupeze M'bale Branham, muzingoimbira ku Chicago. Ngati iye sali kumeneko, chabwino, ndiye muziyimbira ku Shreveport." Ine ndinkakhala kumeneko mochuluka kwambiri.

6 Joseph wachokako ku Chicago. Izo zinaswa mitima yathu, poyamba, pamene ife tinaganiza kuti iye ayenera kuchokako ku Chicago, koma titatha kupemphera ife tinapeza kuti anali Mulungu akumuyitana iye. Ndipo mzanga wamng'ono uyu tsopano wayaka kwambiri mu ntchito yaikulu ku Tanganyika ndi Kenya ndi Uganda, ndipo iye akuchita ntchito yaikulu. Ndipo ife tikumverera kuti timuthandizire iye mwanjira iliyonse yomwe ife tingathe mmisonkhano iyi. Ndipo ine ndikukonzekera, ngati icho chingakhale chifuniro cha Mulungu, mu Januwale akubwerayu, kuti ndikakhale ndi iye mmasukulu ake kudutsa mu Afrika kumeneko, pamene tidzakhale tikupita ku South Africa kuchokera ku masukulu ake. Ndipo iye akuuzani inu zochuluka za izo usikuuno mu zoyankhula zake kwa mpingo. Iye adzakhala akuyankhula ano—madzulo ano pafupifupi, ine ndikuganiza pafupifupi eyiti koloko, mwamsanga zoyambirirazo zikatha. Ndipo kenako iye ali ndi filimu imene mudzakondwera kuyiwonera, ine ndikutsimikiza. Ndipo filimu imeneyo ndi ya masukulu ake a mu Afrika, ndi zimene Ambuye amuchitira iye mu zaka pang'ono zokha. Izo ndi zolimbikitsa kwambiri kwa ine kuwonetsa chimene. . . kuwonera filimuyo, chifukwa iyo ikuwonetsa chimene Mulungu angachite ndi munthu mmodzi amene angapeze chifuniro Chake ndi malo. Atatha kuyembekezera kwa zaka kuti apeze zimenezo, kenako nkumayenda mu njira imene Mulungu anamulondolera

iye. Muwabweretse anawo, gawo loyambirira la iyo ndi gawo laling'ono kwambiri.

7 Monga inu mukumudziwira, Joseph, ambiri a inu, ali ndi chikhalidwe choseketsa. Ndipo ine ndikuganiza iye ankaganiza kuti ine ndikanakhala ndikuyang'ana pa chithunzi chake, kotero iye anapita kunja usiku wina ndipo ankafuna kuti akajambule chithunzi cha mkango. Ku Afrika uko, kuli mikango yambiri. Kotero Joseph anapita kumeneko ndipo anakajambula mkango. Ndipo ine ndinaganiza kuti icho chinali chinthu chokongola kwambiri. Azimayiwo atatha kupha nyamayo, ndipo iwo atatha kudya—nyamayo, iye ankasenda chikopacho. Ndipo mwana wake wamng'ono amatsatira pambuyo pake, kumayesetsa kumachita ngati akuyesetsa kuti ayiphenso iyo kachiwiri, inu mwaona. Ndipo ine ndikutsimikiza kuti ana achichepere asangalala nazo, ine ndikuganiza, maminiti faivi kapena teni a iyo kumayambiriro kwa filimuyo. Tsopano, mubwere molawirira.

8 Ndipo ine sindinafunsidwe kuti ndinene ichi. Ine sindikufuna kunena icho. Joseph sakudziwa kanthu za icho. Koma ine ndikuganiza kuti usikuuno ife tiwonetsera kuyamikira kwathu kwa M'bale Joseph pomupatsa iye chopereka cha ku utumiki wake wa kutsidya kwa nyanja. Ife tikukhulupirira kuti Ambuye Yesu akubwera. Ndipo—ndipo ngati inu mwakhala mukusunga chopereka chochepa chaumishonare, kapena chinachake kwa mamishonare, kapena chinachake chimene inu mungafune kutero, chothandizira kwa izo, mupange cheke chanu kwa Joseph B-o-z-e, usikuuno. B-o-z-e, uko nkulondola, sichoncho izo? Joseph Boze. Ndipo izo ndi . . . Ine ndikumudziwa M'bale Joseph ngati wapa chifuwa, mzanga wapadera, ndipo ndikudziwa kuti izo zidzapita ku Ufumu wa Mulungu, mwa kudziwa kwake kopambana kwa Iwo.

9 Ndipo, kotero, ife tisanapite patali, ine ndikufuna kuti ndimudzutse ndi kumulola iye kuti angokhala ndi mawu apa. Ine ndinayesetsa kumupangitsa iye kuti atenge msonkhano wa mmawa, ndipo iye sanachite izo, kotero iye ayankhula kwa ife usikuuno nthawi ya eyiti koloko, kwa nthawi yomwe iye angaisamalire. Ndipo kamerayo idzaikidwa, ndi powonera pake apa, za chithunzicho. Koma pakali pano ine ndikungofuna kuti ndinene kwa mpingo, ndi kumudzutsa kwa mpingo bwenzi langa labwino ndi m'bale, Joseph Boze. M'bale Boze.

[M'bale Boze akuyankhula kwa maminiti naini—Mkonzi].

Zikomo inu, M'bale Joseph, izo ndi zabwino kwambiri. Ambuye akudalitseni. Iyi ndi Sweden ndi Ireland, pamodzi. Mulungu akudalitseni inu, M'bale Joseph. Zikomo inu chifukwa cha ndemanga zanu, M'bale Joseph. Izo ndi, ine ndikhoza kunena chimodzimodzi za iye. Ndife othokoza kwambiri kwa Ambuye

chifukwa cha ntchito yake yayikulu imene ikuchitika mu Afrika, ndipo iye akuuzani inu zochuluka za izo usikuuno.

10 Ndipo tsopano ine ndikukhulupirira kuti Billy anazembera ndipo anadzandiuza ine kuti M'bale Neville kapena winawake pa . . . Zo—zowulutsira mawu siziri bwino kwambiri kumbuyoko. Kapena mwina . . . Kodi mukukhoza kundimva bwinobwino kumbuyoko? Ayi, iwo sakumva bwino kwambiri. Kodi inu mungakonze makinawo?

11 Ndipo ine ndikukhulupirira, pamene ife tikumuyembekezera iye kuti achite zimenezo, ine ndikukhulupirira kuti msuweni wanga, Donna, ali ndi wamng'ono . . . iye ndi Teddy ali ndi mwana wamng'ono pano amene iwo akufuna kuti amudalitsire kwa Ambuye. Ndipo chotero, Donna, ngati iwe ungamubweretse mnyamata wamng'ono uyu tsopano, bwanji . . . Ndipo, tiyeni tiwone, alikuti mlongo wapa limba, woyimba, kodi iye alipo?

12 [M'bale Edgar Branham akuti, "Gwiritsani ntchito imodzi ya maikrofoni ali pambaliwo, wokondedwa."—Mkonzi]. Awa apa? ["Izo ziribwino."] Chabwino, bwana. ["Aliwonse a iwo afikira."] Izo zikhala zabwino. Chabwino. Ine ndinali . . . Ine ndinali pamalo olakwika. Ine ndikuganiza kuti ndinali ine amene ndinali pamalo olakwika.

13 Tsopano, ife tiri ndi nyimbo yaying'ono imene ife kawirikawiri timayimba pa nthawi yino kwa ana, ndi yakuti, "Abweretseni iwo, abweretseni anawo kwa Yesu." Tsopano mu . . .

14 Mipingo yambiri imawakonkha ana aang'ono awa, ndipo izo ndi zabwino ngati iwo akufuna kuti azichita zimenezo, zimenezo ndi zabwino mosamalitsa mmene ine ndikudziwira. Ndipo ena ali ndi njira zimene iwo, mwinamwake, zimene iwo amazitcha izo ubatizo, ndipo ngati iwo akufuna kuti azizitcha izo ubatizo izo ziri bwino, momwe ine ndikudziwira.

15 Koma Malemba ndi omwe ife timayesetsa kuwatsatira basi momwe Baibulo limanenera izo, kumangokhala mu Lemba. Palibepo malo mu Baibulo, mu Chipangano Chatsopano, koma pamene iwo anawabweretsa ana aang'ono kwa Yesu ndipo Iye anawadalitsa iwo, ndipo anati, "Lolani ana aang'ono adze kwa Ine, pakuti kwa otere uli Ufumu wa Kumwamba." Tsopano, umo ndi momwe ife timachitira izo. Abusa ndi ine timayima pamenepo, timamutenga mwanayo ndi kupereka pemphero lomudalitsira kwa Ambuye. Ndiyeno pamene iwo ali . . .

16 Ife timamverera kuti mwana samakhala ndi tchimo, osaposa tchimo lake limene iye anabadwiramo. Ife tonse tinabadwira mu tchimo, tinawumbidwa mu kusaeruzika, tinabwera mdziko tikuyankhula mabodza. Ndipo, tsopano, pamene Yesu anafa pa Kalvare, Iye anachotsa machimo a dziko lapansi. Ndiye mwanayo akanakhoza kukhala atabadwa, kapena

iye mwinamwake akanakhoza kukhala atafa asanabadwe; kapena kubadwa iye asanafike pa usinkhu wa kuzindikira, iye samakhala ndi machimo. Yesu anachotsa machimo a dziko lapansi. Koma iye akadzakula mokwanira ndikumachita tchimo, ndiye iye akuyenera kudzavomereza machimo ake ndipo kenako nkudzabatizidwa kuloza ku chikhululukiro cha machimo ake, inu mwaona. Koma tsopano, ndithudi, iye ndi wamng'ono kwambiri.

17 Tsopano, tiyeni tonse tiyimbe nyimbo yabwino yakale iyi tsopano, ife tiyimba tsopano. Ine sindikudziwa ngati ine ndingathe kutsogolera kapena ayi.

Abweretseni . . . mkati, abweretseni iwo,
Abweretseni iwo kuchokera ku minda ya tchimo;
Abweretseni iwo, abweretseni iwo,
Abweretseni anawo kwa Yesu.

18 Dzina lake ndi ndani? Teddy, Junior. Chabwino, bwana. Ndife okondwa kwambiri kuwona banja laling'ono ili pano mmawa uno ndi Teddy wamng'ono wabwino uyu apa, ndipo tikupemphera kuti Mulungu amudalitse iye mochuluka, ndi kumupatsa iye Moyo Wamuyaya mdziko limene liri nkudza, ndi moyo wautali kuno. Mungalole ndimunyamule iye miniti yokha? Uyu ndi Teddy Arnold wamng'ono. Ife tonse tikumudziwa Teddy kuno, iye ndi wathu . . . m'bale kuno ku tchalitchi, anakwatira mwana wamkazi wa mchimwene wanga kuno, Donna. Ndipo iwo ali ndi munthu wamng'ono uyu pano, mlendo. Ndikuganiza uyu ndi wachiwiri wanu. Ndipo winayo ndi mtsikana wamng'ono, si kulondola uko? Iye ndi mnyamata wamng'ono wowoneka-mowala. Ine nthawizonse ndimachita mantha kuti ndiwathyola iwo akabwera ali aang'ono chonchi, chotero—ofewa chotero, ndimangowopa kuti iwo athyoka.

19 Tsopano kodi inu mungalingalire mayi akumubweretsa wamng'ono wake monga chonchi kwa Ambuye Yesu? Ngati Iye akanakhala pano mmawa uno, munthu monga ife taimiramu, mayi uyu akanathamangira mwamsanga kwa Iye, kufuna kuti Iye ayike manja Ake pa mwana uyu ndi kumudalitsa iye. Mtima wa Adadi ukanakhoza kulumpha ndi chisangalalo. Ife tikudziwa kuti Mulungu wamupereka uyu ku chilumikizano chawo ndipo iwo akufuna kumubwezera iye kwa Mulungu mwa kumuyamikira Iye pomupereka iye kwa iwo. Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

20 Atate athu Akumwamba, ife tikuyesetsa kutsatira chitsanzo Chanu. Pamene azimayi ndi azibambo anabweretsa kwa Inu ana aang'ono, Inu munayika dzanja Lanu pa iwo ndipo munawadalitsa iwo. Ndipo tsopano, Atate Akumwamba, banja laling'ono ili ladalitsidwa mnyumba yawo, polandira mnyamata wamng'ono uyu, Teddy Arnold wamng'ono, Junior. Chotero ife

tikupemphera, Atate Akumwamba, kuti madalitso Anu akhale pa mwanayu. Ife tikuyika manja athu pa iye pokumbukira Inu ndi lonjezo Lanu kwa ife, kuti ife tiziyika manja athu pa anthu pokumbukira Mawu Anu aakulu. Mumudalitse Teddy wamng'ono. Mulungu, ife tikupemphera kuti Inu mumupatse iye moyo wautali, thanzi labwino. Mulole kuti iye akhale moyo kuti adzawone Kudza kwa Ambuye, ngati izo ziri zotheka. Ndipo ife tikuwapempherera abambo ake ndi amayi, mulole kuti iwo adalitsidwe pomulera mwana uyu. Ndipo ngati kuli mawa, mudzamupange iye kukhala mtumiki, Ambuye, wa Uthenga, ndipo mupereke kwa iye zinthu zimene Inu munalonjeza kwa mtundu wa anthu, kuti iye akakhoze kukhala ndi moyo, ndipo Moyo wochuluka. Ife tikumupereka kwa Inu tsopano, Teddy Arnold wamng'ono, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

21 Mulungu akudalitseni inu, Donna ndi Teddy, moyo wautali ndi madalitso ambiri; ndi kwa iwe, Teddy wamng'ono, chifukwa Iye amakukonda iwe.

22 Oh, ine ndikuganiza kuti iwo ndi okongola kwambiri, ine . . . anyamata aang'ono. Ine ndimawakonda anthu onse, koma ine ndikuganiza kuti ana ndipo, kenako, anthu achikulire, pamene inu mwakalamba. Mwamuna wina wachikulire kapena mkazi amene wabwera pa njirayi, ndipo wofooka kwambiri, ndipo ine ndikuganiza kuti iwo amakhala omvetsa chisoni basi, inu mukudziwa, ndipo ndikungoganiza kuti sitikuyenera konse . . . Mukawaona iwo akuwoloka msewu, muziyima. Nanga bwanji ngati amenewo akanakhala abambo anu kapena amayi anu? Mukuona? Awinawake, chotero muziwalemekeza iwo. Ndipo iwo amayankhula mwinamwake pang'onopang'ono ndi nthawi yaitali, ndipo mwinamwake zinthu zimene inu simumafuna kuti muzizimva, koma, kumbukirani, inu mukhoza kudzakalamba, nanunso, tsikulina, chotero nthawizonse muzingowalemekeza iwo.

23 Ndipo ana aang'ono amenewo, ndani angakhoze kuzunza mmodzi wa iwo? Tiri pomwepo, inu simukuyenera kumachita zimenezo. Inu mukudziwa, Yesu anati, "Samalani kuti musamamunyoze aliyense wa aang'ono awa, pakuti angelo awo nthawizonse amawona nkhope ya Atate Anga amene ali Kumwamba." Kumbukirani, iwo ali naye mngelo. Inu mukabadwa, iye amakhala ndi inu kudutsa mmoyo wanu wonse. Ndipo tsopano, ndiye pamene inu mupulumutsidwa, inu mumakhala ndi Mzimu Woyera ndiye, ndipo Iwo umakutsogolerani inu ndi kukulondolerani inu.

24 Ndipo tsopano ine ndikuyang'ana pa omvetsera kuti ndiwawone iwo amene ine ndikuwadziwa. Ndipo, ngati ine sindikulakwitsa, ine ndikumuwona mlongo wochokera ku Chicago cha kuno; izo zimakupangitsa iwe kumamverera ngati kuti uli kwanu, kuimiriridwa ku Chicago, Mlongo Peckinpaugh ndi onsewo motsatira njirayo kumeneko. Ndife okondwa mmawa

uno kumuwona M'bale ndi Mlongo Cox pano; ndi Charlie, Nellie, monga ife timawadziwira iwo. Ndipo Rodney ali pano penapake, ine ndikuganiza, Mlongo Cox. Ndi M'bale Willard Crase, mmodzi wa abale athu otumikira pano. Ndipo osiyanasiyana ochuluka kwambiri amene sindinathe kuwatchula iwo onse.

25 Ndine wokondwa kumuwona M'bale Evans ndi Mlongo Evans kumbuyo uko. Uyo ndi mwamuna amene ine ndinkakuuzani inu kuti analumidwa ndi mphiri, ndipo Ambuye. . . Kodi inu mungangokweza mmwamba dzanja lanu kapena chinachake, M'bale Evans, kotero kuti iwo athe kuwona mmenemo kuti—kuti a. . . Ife tinali tikuwedza nsomba, ndipo mphiriyo inamuluma iye pa mwendo pomwe. Ndipo ndinayika manja pa iye ndi kumupempherera iye, ndipo iwo sunatupe nkomwe, kapena tinalibenso zochita nazo zitachitika zimenezo. Ndipo Baibulo linati, inu mukudziwa, "Iwo adzatulutsa ziwanda; iwo adzaponda pa mitu ya zinkhanira ndi njoka, ndipo palibe chimene chiti chidzawapweteke iwo; ndipo—ndipo awo. . . mu Dzina Langa, iwo amene akhulupirira pa Ine," zomwe mphamvu zonse ndi zomwe iwo akanati adzachite, ndi zina zotero, zinaperekedwa kwa ife. Ndiye, ngati inu simukungochita mantha!

26 Bwanji ngati winawake atakupatsani inu cheke ndipo nkukhala ndi dzina litalembedwa pansi pa icho, ndipo ngati inu munganyamule cheke chimenecho mthumba mwanu moyo wanu wonse, icho—icho sichingakuchitireni inu ubwino uliwonse. Inu mukuyenera kukatulutsa ndalama ndi icho. Kotero, lonjezo lirilonse mu Baibulo liri ndi Dzina la Yesu lolembedwa pansi pa ilo. Banki ya Kumwamba ili ndi udindo, ndipo zosungidwazo zinaikidwa pa Kalvare pamene machimo athu anakhululukidwa, ife tapangidwa kukhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Ndipo chotero musamachite mantha kukatengako pa mphatso iliyonse imene Mulungu analonjeza. Mungokumbukira, Iye analonjeza izo ndipo izo ndi zanu.

27 Ine ndamuwonapo Iye akuimitsa malawi a moto, akuimitsa magazi, akuthetsa chiwawa cha—cha mdierekezi, ndi kutulutsa adani, ndi kuchiritsa khansa, kuwukitsa akufa pamene adokotala anali atayima pamenepo, atafa kwa maora ndi maora, nkuwuka kubwerera ku moyo kachiwiri. Ine ndaziwonapo izo mu utumiki wanga waung'ono wofooka wa inemwini, nthawi ndi nthawi ndi nthawi. Kotero ine ndawonapo zirombo zakuthengo zikuwetedwa mpaka izo osakhoza kusuntha, ndi zinthu zonse. Kotero Iye ali basi. . . Iye akadali Mulungu. Iye. . . Ngati Iye anayamba wakhalapo Mulungu, Iye akadali Mulungu panobe. Ndipo ngati Iye—ndipo ngati Iye sanakhalepo konse. . . Ndipo ngati Iye sali Mulungu, Iye sanakhalepo konse Mulungu, chifukwa Iye akanayenera kuti akhale. . . Kuti akhale Mulungu, Iye amayenera kukhala wopandamalire, Iye ankadziwa zinthu zonse, Iye ankayenera kuti akhale wamphamvuzonse,

wamphamvu zonse, wodziwazonse, wopezekaponseponse. Ndipo, oh, Iye ndi Mulungu basi! Ungwiro wa ungwiro ndi Mulungu.

28 Tsopano, ine sindikulinga kutero, nthawizina pamene ine ndikuphunzitsa makalasi a Sande sukulu awa ndi pafupifupi foro koloko, Joseph. Kuno ma Lamlungu angapo apitawo, ine ndinakhala pano maora sikisi. Ine sindikufuna kuti ndikuwopsyezeni inu, mwaona. Koma—koma ine sindikutanthauza izo mmawa uno; faivi ndi theka chabe. Ayi. Izi basi . . .

29 Ndikhoza osakhala ndi inu kwakanthawi tsopano, ife tikupita ku Virginia, kapena ku Carolina, ndi Kumpoto ndi Kummwera kwa Carolina, ndipo kenako ku Gombe la Kumadzulo, ndi kukwera ku Gombe la Kumadzulo, ndi kukalowa mu Canada ndi Alaska, ndipo kenako nkudzabwerera. Ndipo mwinamwake, Ambuye akalola, tidzapita ku Africa ndi kukamuwona Joseph, ndi kudzapita kudutsa uko mpaka ku South Africa kachiwiri.

30 Ndipo ndinali ndi msonkhano wopambana osati kale kwambiri mu South Africa, pamene iwo unasintha njira yonse ya Afrika mu maora pang'ono okha, pamene Mulungu, basi mu kuzizwitsa Kwake, kumene nyuzipepala zatsamba loyamba zinalemba nkhanizo, tsamba loyamba lonse ndi lachiwiri ndi lachitatu panalibe kanthu koma nkhani za misonkhanoyo. Woyamba kupita m'menemo, iwo anangomukana, iwo sankakhoza ngakhale kumupatsa munthu mafuta chifukwa iye ankapita ku msonkhanowo, sankawagulitsa iwo kwa iye, ankati, "Aliyense wotengeka monga choncho!" Ndipo tsiku lotsatira, anali wololera kumupatsa iye mafuta a ulele. Mukuona? Kotero ndiko kusiyana kwake basi, inu mwaona. Ndine . . . Chinachake chimachitika. Iye ankaweta kanyama kakang'ono pamenepo, inu mukudziwa, ndipo anati kwa iye, anati, "Kodi iwe ukupita kuti?"

Iye anati, "Ine ndikupita uko ku Johannesburg."

Anati, "Oh, ndinu amuna amalonda?"

31 Anati, "Ayi, ine ndikupita uko kuti ndikamuwone M'bale Branham, ku msonkhano."

32 Anati, "Chiyani?" Anati, "Iwe ukuwoneka ngati munthu wanzeru kwambiri kuposa zimenezo."

33 Iye anati "Chabwino," anati "Ndine Mkhristu. Ine ndikupita kumeneko kuti ndikaziwone zimenezo."

Iye anati, "Ungopita kwinakwakenso ndipo upeze mafuta ako."

34 Ndipo kotero tsiku lotsatira, pobwerera, awo anali malo okhawo oyimapo pakati pa kumeneko ndi ku Transvaal, kotero iye ankayenera kuti adutsire pamenepo, ndipo iye

anayima pa siteshoni yotsatira pamusi pa imeneyo. Ndipo mnyamata ameneyo anathamanga ndipo anamuyitana iye, anati, "Bwera kuno. Bwera kuno." Mapepala onse anali ndi masamba apatsogolo ndi masamba achiwiri, ndi zina zotero, odzaza ndi zimenezo, zimene Ambuye wathu anachita. Ndipo chotero ndife othokoza chifukwa cha zimenezo.

35 Tsopano, mwa kusonkhala pamodzi kwakung'ono chabe, aliyense wa inu amene muli chakuno, amene muli ndi amzanu kuno, tikuyenera kuti tikakhale ku Cow Palace tsopano. Ndi chiwonetsero chachikulu, chiwonetsero cha ziweto cha kumadzulo ku Gombe la Kumadzulo, ku South Gate. Kotero ena a anthu inu ngati ine, amene mumakonda mifuti, ndikadutsa ku Weatherby Factory kumeneko, ndipo mudzapite nane ngati inu mukufuna kutero, ngati mudzakhale kozungulira kumeneko. Ndipo kotero iwo akupita ku malo ochuluka kudutsa mu tsiku, inu mukhoza kudzapita ku Chisumbu cha Catalina, inu mukudziwa momwe izo zimakhalira. Ndipo amuna inu, akazi ndi ana anu aang'ono, Disneyland. Ndipo iye ndi mmodzi wa mamembala a gululo, nayenso, kotero mudzangobwera motsatira. Inu, ine ndikudziwa kuti inu mukakhala ndi nthawi yabwino. Ndipo, pamwamba pa zonsezo, mupemphere kuti Mulungu akatsegule maso a osakhulupirira ndipo akapange otembenuka kwa Khristu.

36 Tsopano ife tiwerenga Mawu ochepa okha kuchokera mu Baibulo apa, chifukwa ine ndimakonda kuchita zimenezi. Ndiyeno ine ndiri ndi Malemba ena ndawalemba apa, mkati umu, ndi cholemba china chimene ine ndikufuna kuti ndiphunzitse mmawa uno, kwa mphindi pang'ono, tikukumbukira msonkhano wa usikuuno. Ndiyeno ine ndikanakonda kuti ndikuuzeni inu zonse zomwe zachitika m'sabata ino mu zoyankhulana zapadera, ndi zina zotero, koma ine ndiribe nthawi. Ndipo ine ndikuzindikira kuti ena a iwo akhala pano mmawa uno, amene akuyembekezerabe pa zokambirana zapadera zimenezo, ochokera kunja kwa mzinda. Ife tiyesetsa kuti tifike kwa iwo sabata ino, mwamsanga . . . tiyesetsa kuti tifikire kwa chirichonse chimene chikudikirira pano, mulimonse, ife tisanachoke.

37 Tsopano ife tikufuna kuti titsegule mu Mauthenga, ku Marko 16, mutu wa 16 wa Marko Woyera. Ndipo mutu wanga lero, wa izi, ndi *Uvangeri Wa M'nthawi Yotsiriza*. Ndipo tiyeni tiyambe kuwerenga pa Marko 16, pafupifupi ndime ya 14.

> Ndipo *atatha kuwonekera kwa khumi ndi mmodziwo pamene iwo anakhala pa chakudya, ndipo anawadzudzula iwo chifukwa cha kusakhulupirira kwawo ndi kuuma kwa* mitima yawo*, chifukwa iwo sanawakhulupirire iwo amene anamuwona iye atatha kuwuka*.

Ndipo iye anati kwa iwo, Pitani inu ku dziko lonse lapansi, ndipo mukalalikire uthenga kwa cholengedwa chirichonse.

Iye amene akhulupirira nabatizidwa adzapulumutsidwa; . . . iye amene sakhulupirira adzalangidwa.

Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira; Mu dzina langa iwo adza*tulutsa ziwanda; iwo adzayankhula ndi malirime atsopano;*

Ndipo *iwo adzatola njoka; ndipo ngati iwo adzamwa chinthu chakupha chirichonse, icho sichidzawapweteka iwo; iwo adzayika manja* awo *pa odwala, ndipo iwo adzachira.*

Kotero ndiye Ambuye atatha kuyankhula kwa iwo, iye analandiridwa kumwamba, ndipo anakakhala pa dzanja lamanja la Mulungu.

Ndipo iwo anapita, ndipo anakalalikira kulikonseko, Ambuye akugwira nawo ntchito, . . . akutsimikizira mawu ndi zizindikiro zikutsatira. Ameni.

38 Pali zochuluka kwambiri zomwe zikananenedwa pa izi. Uku ndi kutuma kotsiriza kumene Ambuye anapereka kwa Mpingo.

39 Ine ndiri . . . ndinapezeka ndikuyang'ana pansi apa. Ine ndikuyesetsa kuganiza . . . M'bale West, ine ndimayesetsa kuganiza za dzina lanu mphindi pang'ono zapitazo, wakhala apo wochokera ku Georgia. Ndipo ine basi sindimakhoza kuganizira lomwe dzina lanu linali, mphindi pang'ono chabe zapitazo. M'bale winayo wakhala apoyo, ine ndikulephera kuganizira dzina lake. Ndipo ambiri a . . . Inu mukumvetsa ine sindikuyesera kuti ndimudziwe pang'ono winawake, koma iwo basi . . . Sindimasunga maina awo mokhazikika basi m'maganizo mwanga.

40 Tsopano ife tikuganizira za uvangeri pa nthawi yotsiriza. Ndipo aliyense amene angatero, angakhoze kuwerenga nyuzipepala, ndi kukhoza kuwerenga . . . Kumwamba kutada ndipo kuli mdima, ndipo mitambo ikubwera mmwamba, ndi— ndi kudziwa kuti ife tikukonzekera kukhala ndi mvula, tikhoza kuimverera iyo mu mlengalenga, ndi kuwona milozo yaikulu patali, ndi kuthwanima ndi kuwomba kwa mphepo, amadziwa kuti tikhala ndi mkuntho, kukhala mvula posakhalitsa. Aliyense amene angakhoze kuwerenga nyuzipepala ndi kuwona zikhalidwe za fuko, mafuko, angazindikire kuti chinachake chikukonzekera kuti chichitike. Pamene inu mumuwona wina ali ndi chidutswa pa phewa lake, ndipo winayo, ndipo iwo akukangana, ali ndi mitundu yonse ya zida ndi zina zotero zoti azimenyana nazo, ndipo popanda mgwirizano, akuvula nsapato zawo ndi kumenya madesiki ndi chirichonse pa misonkhano yawo, inu mumadziwa kuti chinachake chikukonzekera kuti

chichitike. Ndipo izo zimabweretsa pa anthu kukhala ngati kumverera koti chinachake chikukonzekera kuti chichitike. Dziko, monga ife tingatchulire izo, kosmos, dziko lakunja, likumverera kuti kukubwera chiwonongeko, kunena monga kuti m'badwo wa atomiki ukukonzekera kuphulika.

41 Mkhristu akudziwa kuti ndi Kudza kwa Ambuye. Mukuona? Pali chikhalidwe. Zimatengera chimene inu mukuyang'anapo, pakuti Ambuye wathu mosamalitsa anatiuza ife basi zomwe zikanati zidzachitike pa nthawi imeneyo, ndipo ife sitikudziwa miniti kapena oralo, koma tikudziwa kuti ife tikuyandikira chinachake tsopano.

42 Monga ine ndimayankhula kuno nthawi ina kale, ndikuyang'ana pa mwanawankhosa tsiku lina mu Afrika, wochokera ku khola, ndipo iye anali—iye anali akudya mwamtendere kwambiri, ndipo zonse mwakamodzi iye anakhala wamanjenje. Ndipo ine ndinadabwa chomwe chinali vuto ndi nyama yaying'onoyo. Ndipo inu mukudziwa nkhosa siimatha kupeza njira yake yobwererera kulikonse kumene iyo inachokerako, iyo imakhala yotayika kwathunthu. Ndi chifukwa chake Ambuye amatifanizitsa ife ndi nkhosa, mwaona, pamene ife tatayika, pali chinthu chimodzi chokha chimene chingatibwezeretsenso ife, M'busa. Ndipo nyama yaying'ono imeneyi inkalira, ndipo iyo inali itasochera kuchokera ku khola. Ndipo ine ndinazindikira, mu udzu, pansi pomwe, nyama yaying'onoyo sinkatha kuwona icho. Ndipo mwanawankhosa kapena nkhosa sizimanunkhiza mdani wake monga zinazo, monga gwape kapena chinachake monga icho, koma iye—iye ankakhoza kuzindikira kuti imfa inali pafupi. Ndipo apo panali mkango ukubwera ukuzembera, ukubwera mophweka. Iwo unkanunkhiza nkhosayo, kotero iwo unkabwera, inu mwaona, kuti udzagwire mwanawankhosayo. Ndipo nyama yaying'onoyo inali ndi manjenje, ndipo inu simumatha kuwona chifukwa chake, koma iyo inali imfa ikuyandikira kwambiri mpaka iyo inali yamanjenje.

43 Ndipo a—dziko liri mu chikhalidwe cha misala chotero pakali pano mpaka kuti iwo akumayendetsa mu msewu mamailosi nainte pa ora, kuti akakhale ku bala ndi kukamwa kwa maola awiri asanapite kwawo. Ndipo ndiko kuukira kwa . . .

44 Yankhulani kwa winawake, oh, mai, iwo amaphulika! Monga ine ndinali kuyankhula usiku wina ku kachisi, ndipo zokhudza kupita ku chipatala kunja kuno kukayesetsa kuyankha ena a mafoni a M'bale Neville. Ndipo nthawi iliyonse imene ine ndimayankhula kwa namwino kapena dokotala, iwo amatha kukuyankha mokwiya, "Ine sindikudziwa kanthu za zimenezo!"

45 Chabwino, ine ndinaganiza, "Chavuta ndi chiyani? Aliyense akungotulutsa ukali, ine ndikuganiza." Koma, dokotala, azamisala akuwasamalira madokotala azamisala.

46 Kotero, koma pali njira yotulukira, ndiyo Khristu. Tsopano, Mkhristu sakuyenera kumakhala mu chikhalidwe chimenecho. Ife tikuyenera kumakhala okondwa, tikuyembekezera Kudza, pakuti kwayandikira. Ife tikutha kumverera mphepo yozizira ya Kalvare. Pamene ife tiyang'ana pansi ndi kumuwona Mulungu wa Kumwamba Amene anapanga lonjezo, ndi zinthu zomwezo zimene Yesu anazichita mmoyo Wake, analonjeza kuti zikanadzabwerera mmasiku otsiriza, ndipo pano ife tikuziwona izo. Ndi chiyani chimenecho? Umenewo ndi mpweya wa kutsitsimutsa kumeneko, monga mvula ikubwera. Mukuona? Ife tikudziwa kuti chiwombolo chayandikira. Mukuona? Chinachake chikukonzekera kuti chichitike. Tsopano, dziko silikuchiwona icho. Iwo amachiseka icho, chifukwa monga iwo anachitira mmasiku enawo. Koma ife tikudziwa kuti izo zikubwera moyandikira.

47 Ndipo ndi chifukwa chake ine ndinasankha phunziro ili lero, ngati lotsiriza langa kwa kanthawi pang'ono ku kachisi uno, pa uvangeri wa nthawi yotsiriza. Ndipo pamene ife tikuchita ntchito ya umishoni kapena mishoni yakunja, ndi Mawu a Mulungu, ife timadziwa kuti nthawizonse timakhala tiri mu chifuniro cha Mulungu, chifukwa kutuma koyamba kwa Yesu kwa mpingo Wake kunali "Pitani ndipo mukalalikire Uthenga." Utumiki wotsiriza uwu unali woti tizilalikira Uthenga.

48 Nthawi yoyamba imene Iye anayamba wadzozapo munthu aliyense kuti azilalikira Mawu ndi kupita kudutsa mdziko lonse, Iye anati, "Kachiritseni odwala, kawukitseni akufa, katulutseni ziwanda; monga mwalandira mwaulere, kaperekeni mwaulere." Mateyu Woyera, mutu wa 10, akuwatumiza seventewo, awiri awiri. Kumeneko kunali kutuma koyamba kumene Iye anapereka ku Mpingo Wake.

49 Tsopano, kutuma kotsiriza kumene Iye anapereka ku Mpingo Wake basi Iye asanalandiridwe mu Ulemelero, Iye anati, "Pitani inu ku dziko lonse lapansi." Iye anali atangowuka kumene kwa akufa. Ndipo ambiri a iwo anali atakhala pamodzi, ndipo Iye anawadzudzula iwo chifukwa cha kuuma kwa mitima yawo, chifukwa cha kusakhulupirira kwawo, kuti sanawakhulupirire iwo amene anali atamuwona Iye Atatha kuwuka. Mwaona, iwo anali ndi umboni wakuti anawawona Ambuye. Ndipo enawo sanakhulupirire zimenezo, ndipo Iye anawadzudzula iwo chifukwa cha kuuma kwa mitima yawo. Iwo sanawakhulupirire anthu awa omwe anali atawona kuti Iye sanali wakufa, "Iye ali moyo!"

50 Chinthu chomwecho lero, pamene inu muwona ntchito Yake. Tsopano, ife tawona kale ndipo tikuchitira umboni kuwonekera kwa Ambuye. Tsopano kumbukirani, kuwonekera ndi kubwera ndi mawu awiri osiyana, kuwonekera ndipo kenako nkudzabwera. Tsopano ndi nthawi ya kuwonekera, Iye wawonekera kale m'masiku otsiriza ano. Pomwe pano ali nafe

mu zaka zingapo zapitazi. Tsopano, ndi chizindikiro cha Kudza Kwake. Iye akuwonekera mu Mpingo Wake, mmawonekedwe a Mzimu Woyera, kuwonetsera kuti ndi Iyeyo, chifukwa anthu sangathe kuchita zinthu izi zimene inu mumawuwona Mzimu Woyera ukuchita, chotero ndiko kuwonekera kwa Ambuye. Tsopano kumbukirani, ilo linayankhula malo onsewo, "kuwonekera" ndi "kubwera."

51 Tsopano, Iye anawadzudzula iwo chifukwa cha kuuma kwa mitima yawo, chifukwa iwo sanawakhulupirire iwo amene anali ataziwona izo. Ine ndikukhulupirira kuti Iye angachite chinthu chomwecho lero. Ife titatha . . . Iwo a . . . iwo sanakhulupirire umboni wa anthu amenewo, ndipo Iye anawadzudzula iwo chifukwa cha zimenezo. Ndiyeno Iye anawatuma iwo kuti apite mu dziko lonse, akalalikire Uthenga kwa cholengedwa chirichonse, ndipo Iye akanadzakhala ndi iwo mpaka ku chimaliziro, mapeto a dziko lapansi. "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira."

52 Tsopano, lero, ife timayesetsa kuwatengera Mawu olembedwa amene ife tiri nawo mmawonekedwe a zilembo, mawonekedwe a kachikhulupiriro ndi zina zotero, ku dziko lonse. Ndipo pakhala pali amishonare atapita konsekonse. Koma ife timakapeza chiyani tikakafika kumeneko? Mbadwa imene siingakhoze kuwerenga dzina lake, itanyamula kabuku mdzanja lake. Iye samadziwa zochuluka za izo kuposa momwe iye amadziwira lomwe liri dzanja lamanja ndi lamanzere. Koma pamene Yesu anati, "Pitani ndipo mukalalikire Uthenga," Iye sananene konse kuti "mukaphunzitse Mawu." Iye anati, "Mukalalikire Uthenga!" "Ndipo Uthenga sunadze mu Mawu okha, koma kudzera mu kuwonetseredwa kwa Mawu," pakuti njira yokhayo imene izo zikanakhoza kuchitidwa inali kupanga lonjezo Lake kuti likwaniritsidwe.

53 Mnyamata wina akhoza kuwerenga izo ngati mu William Jennings Bryan, pamene iye ankatsutsana ndi Darrow pa mfundo za Darwin. Mukuona? Iye ankakhoza kungonena zomwe Darwin ananena. Ndipo William Jennings Bryan ankanena zimene Baibulo linanena. Umenewo unali mtsutsanowo. Koma, mu nkhani iyi, Mulungu amabwera pakati pa anthu ndipo amatsimikizira kuti Mawu Ake akuwonetseredwa. Ndipo njira yokhayo imene inu mungachitire zimenezo, si mwa kabuku, koma mwa Mzimu Woyera ukugwira ntchito kudzera mwa inu. Moyo wanu umakhala moyo Wake. Iye ali mwa inu.

54 Achikunja, pamene iwo ankapembedza fano lawo, iwo ankadzilambatitsa okha pamaso pa fanolo, ndipo ankakhulupirira kuti fanolo linkayankhula mobweza kwa iwo, kuti mulungu, mulungu wawo amatembenuka, amabwera mu fano ili ndipo ankayankhula mobweza kudzera mwa iwo. Tsopano, zimenezo ndi zotsutsana basi, zimatembenuza chimene Mulungu ali. Mulungu samachita ndi mafano. Inu ndi chida

Chake. Inu mumadzilambatitsa nokha pamaso pa Mulungu, ndipo Iye amabwera mwa inu ndipo amadzayankhula kwa anthu. Ndiko kusiyana kwakeko. Iye ndi Mulungu wamoyo kwa munthu wamoyo, osati Mulungu wakufa kwa fano lakufa. Iye ndi Mulungu wamoyo kwa munthu wamoyo. Ndipo inu mumadzakhala mboni Zake, zimene Iye ananena apa.

55 Ndizo tsopano, zindikirani, anthu ambiri amanena kuti zimenezo zinali za atumwi okha. Iye ananena apa, "Pitani inu ku dziko lonse ndipo mukalalikire Uthenga uwu kwa cholengedwa chirichonse, ndipo" (mlumikizi) "zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira."

56 Tsopano, lero, ife timati membala wabwino wa mpingo amagwirana chanza ndi abusa, amatenga dzina lake kuchokera ku Methodisti nkupita nalo ku Baptisti, kapena kuchokera ku Baptisti nkulipititsa ku Methodisti, kapena zina zotero, ndipo amakhala moyo wabwino kwambiri. Tsopano, ife mamishonare, ife timawaona achikunja amenewo akukhala moyo umene Achimereka awa, otchedwa Akhristu, sangafanizane nawo mwanjira iliyonse. Mukuona? Kotero ngati kungokhala moyo wabwino chiri chimene chimawerengeredwa, iwo ndi opulumutsidwa mofanana ndi ena onse a iwo, mwa fano. Makhalidwe awo angatilefule ife mpaka sitingakhoze kupeza mwayi woyima pamaso pawo, uko nkulondola, ndi machitidwe awo. Koma izo si zimenezo.

57 Yesu anati, "Inu mukuyenera kubadwa mwatsopano." Kuti mubadwe mwatsopano, mukuyenera kudzilola nokha kupita ndi kukafa, ndipo Mzimu wa Khristu nkubwera mwa inu. Ndiye simulinso inu; ndi Khristu mwa inu, mwaona, Mzimu Woyera. Paulo anati, "Ine ndimafa tsiku ndi tsiku; komabe ine ndimakhala moyo, osati ine, koma Khristu amakhala moyo mwa ine." Mwaona, Khristu!

58 Ndipo ngati ine ndikanakuuzani inu kuti mzimu wa John Dillinger unali mwa ine, ine ndikanakhala ndi mifuti pano ndi kukhala wophwanya lamulo, chifukwa umenewo ukanakhala wake—mzimu wake mwa ine. Ngati ine ndikanakuuzani inu kuti mzimu wa wojambula, inu mukanandiyembekezera ine kuti ndizijambula chithunzi cha wojambula.

59 Ngati ine nditakuuzani inu kuti ndine Mkhristu, ndipo Mzimu wa Khristu uli mwa ine, kapena mwa inu, ndiye ife tingamachite ntchito za Khristu. Yesu ananena, mu Yohane Woyera, "Iye amene akhulupirira pa ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita." Kenako Iye ananena apa, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira."

60 Tsopano, kudutsa mu m'badwo, pakhala pali nthawi imene zizindikiro izi sizimawatsatira okhulupirira. Uko nkulondola. Mneneri anayankhula za izo, ndipo iye anayankhula za zimenezo mu Zakariya, iye anati, "Idzafika nthawi imene siidzatchedwa

usana kapena usiku, koma mu nthawi ya kumadzulo kudzakhala kuwala."

61 Tsopano, dzuwa limatuluka kummawa ndipo limakalowa kumadzulo. Ilo silimasintha, ndi dzuwa lomwelo. Tsopano pamene Mzimu Woyera unabwera, Yesu, Mwana wa Mulungu, Iye anabwera kummawa, pa anthu akummawa. Ilo lakhala liri tsiku. . . pamene ilo limayenda, monga chitukuko chayenda limodzi ndi dzuwa, kubwera kuchokera kummawa kupita kumadzulo, ndipo tsopano ife tiri ku Gombe la Kumadzulo. Ife tikapita mopitirira, tibwereranso kummawa. Kotero, chabwino, chirichonse chikuwonetsera Kudza Kwake. Ife tiri pa nthawi yakumapeto. Chirichonse chikusonyeza kuti izo zonse zatha.

62 Tsopano, tsopano mneneriyo anati (Ndipo palibe ulosi ungakhale, ukuyenera kumasuliridwa mwamseri, monga Yesu ananenera; Ndizo ndendende basi zimene Iwo ukunena.): "Kudzakhala kuwala kumadzulo." Ndiye Mwana yemweyo amene anabwera pa anthu akummawa ndi kuwonetsera ntchito Zake ndi madalitso Ake, izo zinaloseredwa kuti kudzakhala tsiku lachimbuuzi; osati usana kapena usiku, limenelo ndi tsiku lolunda, limene liri longa la chifunga. Ndipo iwe sungakhoze kuliwona dzuwa, koma dzuwa limaperekabe kuwala kokwanira. Chinachake monga kuliri kunja uko tsopano, mwinamwake koderako pang'ono. Ndipo ife takhala nazo zokwanira zojowina mpingo ndi kuyika dzina lathu pa mabuku, ndi zina zotero, koma mu nthawi ya kumadzulo mphamvu yaikulu yomweyo ya Khristu ikanadzabwera pa Mpingo Wake chimodzimodzi basi monga momwe iyo inachitira kumbuyo uko kummawa. Kumadzulo ikanadzakhala chimodzimodzi. Kotero icho ndi chifukwa chake ine ndikufuna kuti ndiyankhule pa uvangeri wa nthawi ya kumadzulo.

63 M'badwo uliwonse wakhala uli ndi uthenga wake ndi amithenga ake. Monse kudutsa mu nthawi, m'badwo uliwonse wakhala ukunyamula uthenga wake ndi mthenga. Mulungu, mu kam'badwo kalikonse, wakhala akutumiza winawake wodzozedwa ndi Mzimu Woyera, kuti abweretse Uthenga Wake kwa m'badwo umenewo, nthawi iliyonse.

64 Tsopano, ife tikhoza kuyambira kumbuyo, kuti tiyikire kumbuyo izo pang'ono pokha. Ngakhale kuyambira pachiyambi, Mulungu anali Wamthenga pachiyambi, kuti azimuuza Adamu ndi Eva, "Inu mudzadya *ichi,* koma inu musadzachite *ichi.*" Umenewo unali Uthenga. Ndipo pamene munthu anadzaphonya pa Uthenga wa oralo, izo zinabweretsa imfa ndi chisokonezo kwa mtundu wonse wa anthu. Tsopano, uko ndi kuchuluka kwa momwe Uthenga umatanthauza. Ndipo kumbukirani kuti sikunali chabe kukana kwathunthu kwa zomwe Mulungu ananena, zimene Eva anakhulupirira, kunali kutenga chimene Mulungu ananena ndi kuchipaka penti icho, kapena—kapena kungochitanthauzira icho molakwika

pang'ono, kungowonjezera pang'ono pokha kwa Icho, kapena kuchotsapo pang'ono pokha kwa Icho.

65 Ndi chifukwa chimene ine ndimakhulupirira kuti Mawu ndi Choonadi. Ngati tizikhulupiriro tathu ndi zipembedzo zathu sizimabwera kwathunthu ndi Mawu, ndiye ndi zolakwika. Ndipo ngati Mulungu sakanaloleza, ndipo Mawu Ake nkukhala ofunikira kwambiri, kungowatenga molakwika mawu amodzi okha a Iwo zinayambitsa zonsezo, imfa iliyonse imene inayamba yachitikapo, kuzunzika kulikonse, mwana wolira aliyense, mwambo wa maliro uliwonse, manda aliwonse kumbali ya phiri, ambulasi iliyonse imene inayamba yafuulapo, magazi aliwonse amene anayamba akhetsedwapo, ukalamba wonse ndi kuzunzika ndi mavuto amene ife tinakhalapo nawo, basi chifukwa chakuti Mawu a Mulungu sanawerengedwe molondola, zinayambitsa zonsezi, kodi Iye adzakhululuka izo pa nthawi yotsiriza ngati ife tidzawawerenge Iwo molakwitsa kachiwiri?

66 Kotero, inu mukuona, Chikhristu ndi chinthu chofunikira. Ngati izo zinabweretsa zaka sikisi sauzande izi za mavuto, chifukwa cha Mawu amodzi ogwiritsidwa ntchito molakwika, tsopano ife sitikubwereranso ndi Mawu ena amodzi ogwiritsidwa ntchito molakwika. Izo zikuyenera kukhala ndendende ndi Mawu, popanda kutanthauzira kwa wina aliyense, basi chokhacho chimene Mawu akunena! Anthu ambiri amasonkhana pamodzi ndipo amati zikutanthauza *ichi,* ndipo iwo amavomerezana, ndipo ena amanena *ichi*. Koma Iwo amati, "Ichi ndi Icho!"

67 Ngati Mulungu ati adzaliweruze dziko lapansi ndi mpingo, ndiye mpingo wake ndi uti? Ngati Iye ati adzaliweruze ilo ndi fuko, fuko lake ndi liti? Iye adzaliweruza dziko lapansi ndi Mawu, Baibulo. Pakuti, "Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu." Ameneyo anali Khristu, anali Mawu a Mulungu atapangidwa thupi, oyankhulidwa kudzera mwa munthu.

68 Tsopano, mu Bukhu la Chivumbulutso, Iye anati, "Ngati munthu aliyense ati adzachotse Mawu amodzi umu, kapena kuwonjezera mawu amodzi kwa Ilo, kwa yemweyo lidzachotsedwamo, gawo lake, mu Bukhu la Moyo."

69 Kotero inu mukuona izo si basi, "Chabwino, ine ndimakhulupirira *ichi*, koma ine sindikudziwa za *icho*." Inu mukuyenera kukhulupirira Ilo lonse. Mwinamwake inu mulibe chikhulupiriro choyimira kwa Iwo, koma musamayesere kuima mu njira ya winawake.

70 Ine kawirikawiri ndakhala ndikunena kuti ndikanakonda ndikanakhala ndi chikhulupiriro, pamene moyo wanga udzatha, kuti ndidzapite monga Enoki, osati kufa, koma kudzangoyenda

ulendo wamasana ndi kumapita kwathu ndi Mulungu. Ine ndikanakonda ndikanachita zimenezo. Koma ngati ine ndiribe chikhulupiriro cha mtundu umenewo, Ine sindidzayima munjira ya winawake amene ali ndi chikhulupiriro cha mtundu umenewo. Mukuona?

71 Tsopano, ife tiri mu nthawi ya kumadzulo. Ndipo atumikiwo kutsika kudutsa mu m'badwo. . . Ife tikupeza kuti pa chiyambi pamene mtumiki anatumidwa, kuti—kuti amasulire molakwika Mawu Ake kapena kukayikira Mawu amodzi, uko kunali kuwonongedwa kwathunthu ndi kulekanitsidwa Mwamuyaya kuchoka kwa Mulungu, kumasulira molakwika Mawu a mtumiki ameneyo. Ndipo Mtumiki woyamba anali Mulungu Mwiniwake. Ndipo a. . . Mtumiki wina aliyense wakhala ali Mulungu akuyankhula kudzera mwa munthu, chiyambireni, amene ali Mawu a Mulungu, pakuti panalibe munthu nthawi imeneyo woti Iye aziyankhuliramo koma mmodzi yekhayo amene Iye anali kuyankhula naye. Koma pakuti Iye anamupanga munthu ndipo anamuwombola munthuyo, zakhala ziri Mulungu akuyankhula kudzera mwa munthu. Iye samagwiritsa ntchito—kachitidwe ka—ka makina aliwonse, koma kachitidwe ka munthu, munthu amene ali wodzipereka ndi wodzipatulira kwa Mulungu.

72 Momwe tikhoza kuzitsitsa izo mmusi kudutsa mwa aneneri, ndi Samsoni, ndi kutsika mmusi mpaka mu m'badwo uwu umene ulipo tsopano. Nthawizonse zakhala ziri munthu payekha ndi Mulungu. Tsopano, m'badwo uliwonse, ine ndinati, umakhala ndi uthenga wake ndi wamthenga wake. Tsopano ife titenge m'badwo wina utatha m'badwo wa Edeni, kuti tingopeza maziko pang'ono. Tsopano, utatha m'badwo wa Edeni unabwera m'badwo wa Nowa. Tsopano pamene dziko. . . ife tinali. . . Ine ndimayankhula usiku wina uko ku Clarksville tabernacle, pa phunziro la chizindikiro cha nthawi yotsiriza. Ndiyeno usiku winawo, Lachinayi usiku, pa kuzindikiritsidwa ndi Yesu. Ndipo tsopano mmawa uno pa mvangeri wa nthawi-yotsiriza, uvangeri, mundikhululukire ine.

73 Tsopano, basi chisanachitike chigumula ndi nthawi ya kusefukira, chabwino, ife tikupeza kuti iwo anali ndi chitukuko chachikulu kuposa chimene ife tiri nacho lero. Ine ndikukhulupirira kuti iwo anali ndi ulamuliro wa mphamvu ya atomiki. Ine ndikuganiza kuti icho ndi chimene chinagwedeza dzikoli kuchoka mu kanjira kake. Ine ndayimapo mu British Ice Fields; kukumba pansi mapazi faivi handirede, kutululutsa kanjedza, kumene kunkakhala kanjedza, ndipo mahandirede ambiri a zaka zapitazo. Ndipo ife timaphunzitsidwa ndipo timadziwa kuti dziko linkayima mowongoka. Koma, ndipo iwo anali ndi makina oterowo ndi sayansi yoteroyo mpaka iwo ankakhoza kumanga piramidi, sphinx, zina zotero, zomwe ife sitingakhoze kuzipanga lero. Ife tiribe makina onyamulira miyala imeneyo mpaka pamenepo, mwaona, pokhapokha

itakhala atomiki; mphamvu ya mafuta siyingachite zimenezo, ndipo mphamvu ya magetsi siyingachite zimenezo. Koma iwo unali m'badwo wina wanzeru kwambiri kuposa m'badwo wathuwu.

74 Ndipo mu m'badwo umenewo, Mulungu anamuitana munthu wotchedwa Nowa, munthu wamba chabe, mlimi, chifukwa iye anapezeka kukhala waumulungu mu m'badwo wakewo. Ndipo Mulungu anachita ndi munthu mmodzi ameneyo pa phunziro la "kumanga chombo," chifukwa, tchimo, ife tikuzindikira kuti mu nthawi imeneyo kuti "Ana aakazi a—a anthu," Baibulo linati, "anawona . . . ana aamuna a Mulungu anawona ana aakazi a anthu."

75 Pokambirana izo, ambiri a olemba amaganiza kuti amenewo anali ana aamuna a Mulungu amene angelo akugwa anadzikanikizira okha mu mzimu. Ine sindikuwona momwe munthu angaganizire zimenezo. Izo zingamupange iye kukhala mlengi, kumupanga Satana kukhala mlengi. Satana si mlengi, Satana ndi wopotoza wa chirengedwe, mukuona, zonsezo. Bodza ndi choonadi chitakambidwa molakwika. Chigololo ndi mchitidwe wolondola utachitidwa molakwika. Mukuona? Ndipo ndizo ndendende chimene tchimo liri. Satana sangalenge, iye akhoza kungopotoza chimene chalengedwa.

76 Kotero iwo anali ana aamuna a Mulungu, amene anali ana a Seti ochokera ku mzere wa Mulungu, kudzera mwa Adamu; ndipo ana aakazi a Kaini, Satana, "Ndipo pamene iwo anawona kuti iwo anali okongola, owoneka bwino."

77 Ndipo ife tikuzindikira mmenemo, pobweretsa zithunzi monga za zaka zingapo zapitazo, monga zaka handirede zapitazo, momwe kukongola kwa akazi kwapitiririra kukongola kumene kunkakhala mwa akazi. Ngati inu mungawerenge Genesis 6, inu mupeza chithunzi chokongola cha izo pamenepo. Iwo anali okongola. Ndipo akazi lero ndi okongola kwambiri kuposa momwe iwo ankakhalira. Ndi chifukwa cha mavalidwe awo ndi kachitidwe kawo kamakono. Icho ndi chimene chimawasintha iwo.

78 Ine ndiri ndi chithunzi cha Pearl White, chinali pamene Scott Jackson anamupha iye, analowetsa mpeni mu chifuwa chake, wachikondi wachinsinsi, ndipo fuko lalikulu linagwedezeka ndi nyimbo ya Pearl White. Iye ankayenera kukhala mkazi wokongola kwambiri yemwe analipo mdziko m'masiku amenewo. Bwanji, iye angakhale wamakedzana pa msewu lero, kwa ena a akazi awa.

79 Kapena, kubwerera ku nthawi ya Clara Bow, pamene iye anayambitsa kuyaluka kotsitsira masokosi ake pansi pa maondo ake, ndi kumati, "Atsitseni iwo, atsikana, atsitseni iwo." Ine ndikukumbukira zimenezo mu m'badwo wanga woyambirira.

Ndipo mutenge chithunzi cha Clara Bow ndipo muchifanizitse ndi ena a okongola a lero. Mukuona?

80 Ndipo chimenecho ndi chizindikiro cha nthawi yotsiriza. Yesu anati, "Monga izo zinali mmasiku a Nowa, chomwechonso izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu." Ndipo iwo mopitiriza akumadzivula okha. Ndi chiyani chimenecho? Ana aakazi a Kaini. Icho ndi chifukwa chake ife timatengedwa ngati zidempete ndi otentheka pamene ife tiyesetsa kufotokoza ndi kunena choonadi cha Uthenga pa izo. Koma iwo amangodziyipitsa okha mosalekeza ndi kupita m'misewu ndi—ndi kumachita momwe iwo amachitira, ndipo samazindikira kuti adzayankha pa Tsiku la Chiweruzo. Tsopano, mkazi amene amadziveka yekha molakwika, mwachigololo, ndipo inu mukhoza kukhala wangwiro monga kakombo kwa mwamuna wanu, kapena kwa wokondedwa wanu, bwenzi lanu, koma wochimwa akamadutsa mu msewu ndipo ndikuyang'ana pa inu ndipo inu mutavala mwanjira imeneyo, iye adzakusirirani inu chifukwa inu mwadzipereka nokha kwa iye mwa njira imeneyo.

81 Si ana amene akusowa kukwapulidwa, ndi abambo ndi amayi, chifukwa chowalola iwo kuti azichita monga chomwecho. Uko, si kulekelera kwa ana, ndi kulekelera kwa makolo. Ndipo ine ndikuganiza kuti nkulekelera kochuluka kwa paguwa, pakuti iwo amangowalola iwo kuti azipitirira ndipo osanena kanthu za zimenezo, pamene izo ziri mu Mawu.

82 Tsopano, tsopano Baibulo, Yesu anati, "Aliyense amene adzayang'ana pa mkazi ndi kumusilira iye, potero," tensi yakale, "wachita chigololo ndi iye mu mtima mwake, kale." Ndipo pamene wochimwa ameneyo adzapita ku chiweruzo kuti akayankhire pa chigololo, izo zidzawulukira mmbuyo, "Kodi iwe unachita izo ndi ndani?" Ndi inuyo! Ngakhale inu simunachitepo mchitidwewo, koma Baibulo linati ndinu wolakwa, mulimonse. Ndi ndani woti ayimbidwe mlandu pamenepo? "Aliyense amene ayang'ana pa mkazi kuti amusilire iye, wachita naye kale chigololo mu mtima mwake." Kutsimikiza kwake kwa zimenezo!

83 Mu Jeffersonville lero, muli nainte-naini ndi mateni nainte-naini peresenti ya akazi amene ali olakwa pamaso pa Mulungu. Fuko lonse liri mwanjira imeneyo. Bwanji? Kulekelera pa guwa, kuti awauze anthu; ndi kulekelera kwa pakhomo, kumawalola madona aang'ono kuti azipita pa msewu ndi kumakachita monga chomwecho. Ndipo iwo amazitcha izo "zabwino bwino."

84 Tsopano, ndizo ndendende zomwe Nowa ankayenera kuti azimenyana nazo mu tsiku lake. Ana aakazi a anthu anali okongola, ndipo ana aamuna a Mulungu anayang'ana pa iwo. Mwaona, kusilira kukubweranso. Koma Nowa, oh, ife tikhoza kukhala pamenepo kwa maora. Koma Nowa anali mwamuna wa chirungamo, waumulungu, woonamtima, ndipo iye anafuula motsutsa zoterozo. Ndipo iwo anamutcha iye munthu

wopenga. Onyoza, Baibulo linanena, kuti iwo anamunyoza iye, kummusereula iye. Koma iye anati, "Ikubwera nthawi imene nkuntho, madzi adzagwe kuchokera mu mlengalenga." Panali isanakhalepo mvula. Ndipo Uthenga wake sunagwirizane ndi mfundo zawo za sayansi za tsiku limenelo, pakuti munalibe mvula mu mlengalenga.

85 Ndipo, lero, lingaliro la sayansi la otchedwa magulu achipembedzo amakono layesetsa kutsimikizira kuti Chinthu chodala ichi chimene ife tiri nacho, chotchedwa Mzimu Woyera, ndi kutengeka chabe. Mwaona, izo sizikugwirizana basi ndi mfundo zawo zasayansi. Chabwino, ine ndikufuna kuti ndiwafunse iwo ichi, nchiyani chimawapangitsa iwo kusintha? Kodi nchiyani chimapangitsa chidakhwa kusiya kumwa? Nchiyani chimapangitsa hule kusiya moyo wake woyipa? Nchiyani chimapangitsa khansa ndi—matenda kuchoka kwa anthu, ndi ogontha, osayankhula, ndi akhungu, ndi akufa kuti awuke? Tafotokozani zimenezo. Ndi kutengeka kumeneko? Izo zimakhala nako kutengeka, ndithudi.

86 Chirichonse chimene chiri cha moyo chimakhala ndi kutengeka, ndipo chirichonse chimene chiribe kutengeka ndi chakufa. Mundikhululukire kafotokozedweko, koma ine ndikuganiza kuti ife tikuyenera kuti tikwirire zina mwa zipembedzo zathu zopanda kutengeka ndiye, chifukwa izo ndi zakufa. Izo ziribe kutengeka kulikonse kwa izo. Chipembedzo chirichonse chimene chiribe kutengeka chikuyenera kukwiriridwa, uh-huh, chifukwa, Icho chimakhala chotengeka!

87 Yesu, pamene Iye analowa mu mzinda, ana ndi onse a iwo, abwenzi Ake onse, ankafuula, "Hosanna! Iye amene akudza mu Dzina la Ambuye!" Ndipo achipembedzo amenewo a tsiku limenelo sankatha kupirira nazo, zinali zotengeka kwambiri. Iye anati, "Ngati iwo akhale chete, miyala iyamba kufuula nthawi yomweyo." Mukuona? Chinachake chikuyenera kufuula, chifukwa moyo unali pamenepo.

Nowa anali ndi nthawi yovuta, koma potsiriza tsiku lina iye anali ndi yesero.

88 Ndipo onse amene amapita ndi Mulungu amakhala ndi mayesero, chikhulupiriro chanu chimayesedwa. Pamene inu muyamba kumukhalira moyo Iye, ndiye woyandikana naye aliyense aziyankhula za inu, chirichonse chizipita molakwika kwa inu. Muzingokumbukira zimenezo, pakuti ndi Mulungu akukuyesani inu. Baibulo linati, "Mwana aliyense amene adza kwa Mulungu akuyenera kutsimikiziridwa poyamba, kulangidwa, kuphunzitsidwa monga mwana." Monga bambo anga ankandiphunzitsa ine pamene ndilakwitsa, iwo anali—iwo anali ndi—malamulo khumi atapachikidwa pamwamba pa chitseko, iyo inali nthambi pafupifupi yotalika *chonchi*;

ndipo Bambo Branham anali mwamuna wamphamvu kwambiri mu nkono wake, ndipo iye ankatitengera ife kunja ndipo iye ankakatiphunzitsa ife. Ndipo umo ndi momwe Mulungu amachitira. Iye amayesetsa, amakuphunzitsani inu monga mwana, amakulerani inu, chifukwa ndinu mwana Wake; kuli chinachake mtsogolo kwa inu, kwanu mu Ulemelero. Ndipo Iye amakuphunzitsani inu. Tsopano, mwana aliyense wobwera amayenera kuti ayesedwe.

89 Nowa, choyimira tsopano cha nyengo yake, anali ndi yesero, chifukwa Mulungu anamuuza iye kuti alowe mu chombo, ndipo pamene iye analowa mu chombo, chitseko chinadzitseka chokha. Ndipo Nowa mosakayika anawuza banja lake, "Muwone mawa. Oh, chitseko chatsekedwa usikuuno, koma mmawa mudzakhala mvula mmwamba umo mu mlengalenga." Inali isanagwepo mmuyomo, kumbukirani.

90 Ndipo onyozawo, mwinamwake ena a iwo okhala ngati okhulupirira mwatheka, anati, "Tiyeni tipite uko ndipo tikayime. Inu mukudziwa, bambo wachikulire uja akhoza kukhala kuti amalondola." Iwo anayima mozungulira chombocho, akuyembekezera, inu mukudziwa, ndipo anaganiza, "Chabwino, tsopano, iye akhoza kukhala kuti amalondola." Ndipo iwo anapita mmwamba. Ndipo mmawa wotsatira, dzuwa linatulukira mokongola basi, linadzadutsa.

91 Inu mukudziwa, ndipo sindikukaikira kuti Satana anayima pamwamba apo pamwamba pa bowo ilo mu chombocho, zenera lija, anati, "Iwe ukuganiza kuti ukulondolabe?" Chabwino, umo ndi momwe mdierekezi amachitira ndi tonsefe. Koma bola ngati Mulungu ananena chomwecho, muyime ndi Icho! Zimenezo ziribe kanthu, mukhalebe ndi Chimenecho.

92 Tsiku lachiwiri linadutsa, tsiku lachitatu linadutsa. Nowa ankatuluka thukuta chifukwa cha izo. Koma, potsiriza, atatha masiku seveni! Ndipo apo panali pa 17 Feburuwale pamene iye anadzalowamo. Ndipo kenako atatha masiku seveni, ndiye mmawa umenewo pamene iye anadzuka, mabingu ankabangula, madontho aakulu a mvula ankagwa pozungulira. Iwo amene anabwera ndi kudzakhala kwa tsiku limodzi kapena awiri, kuti adzafufuze, kuti, "Chabwino, ife tipita ndipo tikawona ngati chirichonse chiti chichitike," nthawi inali itatha kwambiri pamenepo. Iwo anagogoda, iwo anafuula. Misewu inadzaza ndi madzi, anayamba kukwera mpaka ku mapiri. Anthu anapita ku zitunda. Iwo anayesetsa kuwakweza iwo mmabwato, ndi zina zotero, koma ngati bwatolo silinamangidwe ndi Mulungu, kugwedeza kwakukulu kwamphamvu kumeneko kwa dziko lapansi pa nthawi imeneyo kunangogwedezera ilo pansi pa madzi.

93 Inu mukuti, "Aliyense! Basi ngati ine ndiri ndi chipembedzo, izo zikhala bwino." Ayi, izo si choncho. Icho chikuyenera

kukhala chokuchitikira chopangidwa ndi Mulungu mu chipembedzo. Mukuona? Zina zonsezo zidzafa. Ine sindikunena izi kuti ndikhale wotsutsa. Ine ndikungonena izo chifukwa cha chikondi, ndi podziwa kuti ine—ine ndikuyenera kuti ndidzayankhe pa tsiku limenelo, ndi kudzayankhira. Kotero ngati ine nditangonena zimene Iye akunena, ndiye ndidziwa kuti ziri bwino. Koma ngati ine nditamayesera kuyika kachikhulupiriro ka winawake kapena lingaliro mu izo, ine—ine sindingakhoze kuchita zimenezo, ine ndiribe chikhulupiriro mwa izo. Ine ndimangokhulupirira zomwe Iye ananena.

94 Tsopano zindikirani, patapita kanthawi iwo anafika pokuya kwambiri, ndipo mpaka mmwamba kwambiri. Iwo anagogoda pakhomo, iwo anafuula, iwo analira. Izo sizinachite ubwino uliwonse. Mwinamwake masiku angapo zisanachitike, pamene iwo ankayika zinyamazo mmenemo, ine ndikanakhoza kuwamva ena a onyozawo akuti, "Lowani mmenemo ndi zinyama zanu zonunkhazo. Zikhalani ndi kununkha kwanu konse mmenemo ngati inu mukufuna kutero."

95 Izo ndi lero basi, iwo amakuuzani inu chinthu chomwecho. "Zipitirirani, kakhaleni akachitidwe kachikale ngati inu mukufuna kutero. Ife tizikhala ndi zisangalalo zathu." Kazipitirirani, mulole izo zizipita. Koma, oh, m'bale, kuti akhale otetezeka mu Chombo, chitsekocho chinatsekedwa! Icho, ndicho chinthucho.

96 Koma Nowa, mu tsiku lake, izo zinali zovuta kwa iye mu nyengo yake, mwaona, chifukwa chakuti anthu anali asanamvepo za chinthu choterocho, koma icho chinadzabwera chimodzimodzi basi. Ndiye ife tikupeza pa chochitikacho, zomwe zinabwera motsatira chiwombolo cha Nowa ndi zina zotero, ndipo dziko lapansi linayamba kumera kachiwiri, ndipo—ndipo chirichonse chimene chinkapuma mpweya chinawononge ka. Ndipo kenako ife tikupeza kachiwiri kuti panadza nthawi, imene, Mulungu ankawatulutsa ana Ake kuchokera ku Igupto, kuti Mose anadzabwerapo ndi chilamulo. Izo zinali zovuta kwambiri kuti anthu amvetsetse, koma nyengo inali ikusintha kufika ku chilamulo. Ndiyeno lamulo litabwera, Mose akuyesetsa . . . Ilo linali mphunzitsi wa sukulu. Anthu ankangokhala mwanjira iliyonse yomwe iwo ankafunira kutero, chotero mphunzitsi wa sukulu, lamulolo, linali, Baibulo linati, kuti awabweretse anthu kuti azindikire kuti izo zinali zolakwika, chotero Iye anawapatsa iwo Malamulo Khumi. Uko kunali kusintha ndithu, anthuwo sanafune kulandira izo. Chabwino.

97 Ndiye atachoka Mose, kunadzabwera Yohane. Ndipo atachoka Yohane, nyengoyo inadzabwera, iye anamudziwitsa Yesu. Ndipo pamene Yesu anabwera kudzayesetsa kutibweretsera ife chisomo, chimene chinali Mulungu mu Mzimu, mu mzere wa Mzimu, anadzawonetsera chikondi

Chake, "Pakuti Mulungu analikonda dziko lapansi mwakuti Iye anamupereka Mwana Wake wobadwa yekhayo," ndipo Yesu anali wosiyana kwambiri ndi wotsutsana ndi lamulo, mwaona, koma iyo inali nyengo yosiyana, nthawi yosiyana.

98 Ndiyeno pamene Yesu anadzachoka, Iye anayankhula za nyengo iyi ya Mzimu Woyera, Moyo mkatimo, Mboni ya Iye ya chiwukitsiro. Ine ndiri ndi Malemba ambiri apa, koma ine ndiribe basi nthawi yoti ndilowe mwa iwo, ine ndingowadutsa iwo mwachidule. Chabwino. Icho nthawizonse chakhala chiri choona ndi—nkhondo, pamene nyengo imodzi ikusintha kuchokera ku nyengo yakale kupita ku Uthenga wanthawi imeneyo, nthawizonse imakhala ili nkhondo ndi anthu. Iwo—iwo—iwo . . . Ndizo, ngakhale nthawizonse zimakhala Mwamalemba. Koma pa nthawi imene Mulungu akuwapatsa iwo nyengo ndi chinachake choti azikhalira nacho moyo, kapena chinachake choti azichita. Tsopano ife tikupeza kuti mwamsanga pambuyo pa kuperekedwa kwa nyengo imeneyo, anthu a pa dziko lapansi amayesetsa kuti apeze chinachake choti chitsutsane ndi icho, ndi chinachake choti apange chopangidwa ndi munthu pa icho.

99 Nowa atatha kukhala ndi chombo, ndipo kenako mwamsanga zitachitika zimenezo, Nimrodi, chigawenga chija, iye anadzamanga nsanja, ndipo anati, "Ngati chigumula chingabwere, ife tidzangokwera mmwamba ndi kukwera pamwamba pa icho." Ndipo zitatero Mulungu anabwera motsatira ndi lamulo limene basi . . . Mwaona, nyengo imeneyo inali itakhala nthawi yake mokwanira.

100 Ndipo pamene Yesu anabwera, nayenso, pambuyo pa lamulo, lamulo linkayankhula za Mose ndi . . . linkayankhula za kudza kwa Khristu. Koma pamene Iye anadzabwera, iwo anali atakhazikika kwambiri mu miyambo ya makolo, iwo anali ndi tizikhulupiriro tawo, iwo anali ndi mafashoni awo, iwo anali ndi mipingo yawo, iwo anali atakhazikika, chotero izo zinali zovuta kwambiri kuti Yesu ayesetse kuwugwedeza ufumu umenewo (mpingo umenewo) kuchoka ku kachikhulupiriro, kuti umukhulupirire Iye. Ndipo komabe Malemba makamaka amayankhula za Mmodzi uyu njira yonse kuchokera ku nyengo yoyamba ya Edeni, "Mbewu Yake idzavulaza mutu wa serpenti." Amalonjeza Yesu kudutsa iliyonse ya nyengozo, ndipo, pamene Iye anadzabwera, iwo sanamuzindikire Iye, chifukwa iwo anali atamangidwa kwambiri mu kachikhulupiriro kawo. Komabe icho chinali choonadi cha Mwamalemba. Mtumiki aliyense ndi Uthenga wake ankalosera za wotsatira pambuyo pake, nthawi iliyonse. Mose, aneneri ananeneratu, Mose ananeneratu za kudza kwa Yesu. Mose anati, "Ambuye Mulungu wanu adzautsa Mneneri wonga ine." Ndi nthawi zingati zimene ife takhala tikudutsa mu zimenezo mu Mauthenga athu kuzungulira dziko lapansi, kuti Mesiya wakudza anali woti adzakhala Mneneri!

101 Ndi chifukwa chake mkazi wa mbiri yoyipa uja, motsutsana ndi atumiki onse aja, iye anakhulupirira Uthengawo. Mkazi wa ku Samariya, pamene Yesu anali kuyankhula kwa iye, Iye anati, "Ndibweretsere Ine akumwa."

102 Iye anati, "Inu mulibe chinthu choti mutungire. Si mwambo wake kuti Inu mundipemphe ine, mkazi wa Chisamariya." Ndipo kukambiranako kunapitirira.

Kenako Iye anati, "Pita ukamutenge mwamuna wako ndipo mubwere kuno."

Iye anati, "Ine ndiribe aliyense."

103 Anati, "Izo nzoona, iwe wakhala nawo faivi, ndipo amene iwe ukukhala naye tsopano si wako."

104 Iye anati, "Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndi Mneneri. Tsopano, ife tikudziwa kuti kukubwera kusintha kwa nyengo. Pakubwera Mmodzi Amene ati adzadzozedwe, yemwe akutchedwa Mesiya, Khristu wa Mulungu, ndipo, pamene Iye adzabwera, Iye adzakhala Mneneri ameneyo." Ndi mochuluka bwanji momwe mkazi ameneyo ankadziwira kuposa alaliki onse a tsiku limenelo! Inde. Ndipo iye mu chikhalidwe chakecho, mwaona, iye anamvetsa Lembalo. Komabe, mkazi wamng'ono wosauka, wokwatiwa ndi amuna asanu, ndipo akukhala ndi wachisikisi, ndipo komabe iye ankadziwa zochuluka za Malemba, chifukwa iye anawatenga Iwo basi mwa mtengo Wake. Ndipo anati, "Pamene Iye adzabwera, Iye adzakhala Mneneri."

Kodi Yesu ananena chiyani kwa iye? "Ine ndi Iyeyo."

105 Ndipo iye anasiya mtsuko wake wamadzi ndipo anathamangira mu mzinda, anati, "Bwerani, mudzamuwone Munthu Amene wandiuza ine zinthu zimene ine ndazichita. Kodi ameneyo si Mesiya yemweyo?" Mukuona? Ndi Iyeyo.

106 Tsopano, mwaona, iye—iye ankadziwa kuti Iye anali akubwera, chifukwa aneneri ndi Malemba anali, mmasiku a Mose, ndi masiku a aneneri, ndi njira yonse mmbuyo mu iliyonse ya nyengo zimenezo, anali atanena, "Iye adzakhala pano, ndipo ichi ndi chimene Iye ati adzakhale!" Oh, mai!

107 Ngati anthu angakhoze kokha kuziwona zimenezo lero, ndiye iwo angadziwe tsiku limene ife tikukhalamo. Iwo angawone kuti ndi lonjezo la Mulungu la tsiku lino. Mulungu anati izo zikanadzakhala mwanjira iyi. Palibe kanthu kolakwika, koloko yaikulu ya Mulungu ikugunda chimodzimodzi basi pa nthawi yoyenera. Ndipo, ngakhale molingana ndi sayansi, ndi maminiti atatu kuti tifike pakati pa usiku. Chotero, inu mwaona, kukanthako kukhoza kubwera nthawi iliyonse. Ndipo izo zakhala ziri zaka ziwiri kapena zitatu zapitazo chinenereni zimenezo. Mwaona, ife tiri pa nthawi yotsiriza. Koma, inu mukuona, ife tasintha nyengo

kuchokera ku m'badwo wa mpingo wakale wa kumbuyo kuno kumene tsiku la chimbuuzi lija linali, kungojowina tchalitchi ndi kulemba dzina lako pa bukhu; kufikira Kuwala kwa kumadzulo, kubwezeretsa, kubwereranso kachiwiri kwa Mzimu Woyera pa dziko lapansi, pentekoste ina, chizindikiro china, chinthu china chinali choti chichitika. Ndipo anthu sakukhulupirira Iwo, chifukwa iwo akhazikika kwambiri monga iwo anachitira mmasiku a Yesu. Mukuona? Iye ananena za tsiku lino. Pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, Iye anabwera ndendende molingana ndi Lemba; kenako Iye ananeneratu za kubwera kwa tsiku *ili*.

108 Tsopano, tsopano ife tikufuna kuti tiganizire za wina apa. Ine ndiri. . .Ngati inu mukufuna kuwerenga ena a iwo, Mateyu 24. Yesu anakamba za tsiku lino, Iye anati Ayuda adzasonkhananso kachiwiri pa tsiku lotsiriza. Iye anati, "Pamene inu mudzawona mtengo wa mkuyu ukuyamba kuphukira, ndiye mudzadziwe kuti nthawi ili pafupi." Iye anati, "Padzakhala kudodometsa kwa nthawi, kupsyinjika pakati pa mafuko, nyanja ikubangula; amuna kumalephera ndi vuto la mtima, mowirikiza." Izo siziri pakati pa akazi, tsopano. Izo ziri pakati pa amuna. Yesu sananene konse kuti akazi; "amuna." Tayang'anani pa mliriwo! Ndipo mu tsiku limenelo chimene chikanati chidzachitike! Chimenecho chikanadzakhala chizindikiro cha nthawi yotsiriza, "Mitima ikulephera, mantha, kudodometsedwa." Vumbulutso, pamene Ilo linayankhula, mneneri akuyankhula za tsiku lino, iye ananena kuti ikanadzafika nthawi imene mpingo ukanati udzakhale wofunda, M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya mmasiku otsiriza. Mukuona? Ndi chiyani chimenecho? Ndi Yesu (m'badwo wotsiriza) akuneneratu za mapeto a m'badwo uno.

109 Chimodzimodzi basi monga mu Edeni, monga uko mu nthawi ya Nowa, ndi mmusi mu nthawi ya Mose, kumatsika mu nthawi ya lamulo—lamulo, ndipo kenako mu nthawi ya chisomo, ndipo tsopano mu nthawi ya kumadzulo. Alipo ena ambiri pamenepo ngati ife—ife tikanakhala nayo nthawi, koma ine ndangowadumpha iwo chifukwa ife sitikhala ndi nthawi. Za wina aliyense akunena chimene chikanati chidzakhale mu m'badwo wotsatira, koma mpingo umakhala wachi tchalitchi ndi tizikhulupiriro tawoto, ndi miyambo yawo, ndi zodzipangitsa kukhulupirira zawo ndi mbalume zawo zopangidwa ndi anthu, mpaka iwo amawaphonya Mawu amenewo. Tsopano inu mukhoza kuwona chimene uvangeri wa m'nthawi ya kumadzulo uti udzakhale. Mukuona? Ndi chiyani chimenecho? Iwo amene ati azidzawuchita Iwo azidzatchedwa amisala. Iwo adzakhala osiyana kwambiri! Iwo analipo mu nthawi ya Nowa, iwo amakhalapo mu nthawi iliyonse. Amachotsedwa mmatchalitchi awo chifukwa ankamukhulupirira Yesu, aliyense amene ankakamumvetsera

Iye ankayenera kuchotsedwa ku mpingo wawo. Mukuona? Koma Iye anali ndi nyengo imeneyo, imeneyo inali nthawi Yake, nyengo ya Mwana.

110 Tsopano, ife tikupeza aponso kuti Mzimu Woyera wawukulu unaneneratu za zimenezo. Inu mukufuna kuti mulembe ena a Malemba awa, Mateyu 24, ndipo kenako mulembe Timoteo Wachiwiri 3:1. Mzimu Woyera ukuyankhula za m'badwo waukulu waluntha pa nthawi yotsiriza. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Nchifukwa chiyani izo ziri chomwecho?

111 Joseph, iwe wayenda ndi ine mochuluka muno mu fuko ndipo iwe wamvapo za misonkhano ya kutsidya kwa nyanja. Ine ndimapita kutsidya kwa nyanja ndipo ndimakakhala ndi handiredi fifite, thuu handiredi sauzande, faivi handirede sauzande, ndipo anthu basi . . . Chinthu chimodzi chabe, chimene inu mumachiwona chikuchitidwa tsiku lirilonse, pamene misonkhano ikupitirira, pafupifupi, muno mu kachisi; mpaka teni, twente ndi sarte sauzande amagwa pa mapazi awo . . . kuchokera pa mapazi awo, kuti apereke matamando kwa Mulungu. Iwo amachiwona Icho. Vuto ndi chiyani, bwanji sizimachitika mu Amerika? Ndi nthawi yaluntha. Iwo amafuna winawake amene angathe kuyankhula osati za chiweruzo, osati za zinthu izi, chifukwa izo zimawaphwasula iwo kuchoka ku chiyanjano chawo ndi makalabu awo ndi—ndi maloji awo, ndi—ndi zinthu zopanda umulungu zomwe iwo alimo. Chotero, ngati abusa awo angatchule chinachake chonga ichi, gulu la madikoni likhoza kumuchotsa iye, ndi kuyikapo winawakenso, Ricky wina wamng'ono kapena chinachake. Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza.

112 Ine . . . Mukhululuke zimenezo, mwaona, ine—ine sindimatanthauza zimenezo, mwaona, koma ine nthawizina ine ndimatengeka kwambiri, ine ndikuganiza. Koma ine ndikutanthauza . . . Ricky ndi zabwino bwino. Ine sindimalikonda basi dzinalo, uko nkulondola. Koma mukakayang'ana ilo mu ziwerengero, inu mukhoza kumusintha dzina mwana wanuyo. Inde, bwana. Tsopano, Ricky kapena Elvis, kapena chinachake chonga chimenecho, oh, chifundo! Chotero, oh, mulimonse, tsopano, inu mwaona iwo amayenera kutero. Iwo analibe maina amenewo m'mbuyomo, iwo akuyenera kubwera. Uno ndi m'badwo woti iwo akhale pano. Ndithudi. Kulondola ndendende.

113 Tsopano, "Ndipo tsopano Mzimu ukunena." Tsopano mvetserani, ine ndikubwereza kwa inu kuchokera mu Lemba.

> *Tsopano Mzimu* ukuyankhula momveka*, kuti mu nthawi za mtsogolo,* mwaona*, nthawi zamtsogolo ena adzachoka ku chikhulupiriro, posamalira mizimu yodolola, . . . ziphunzitso za ziwanda;* ndi zina zotero, mwaona.

114 Taonani momwe iwo akanati adzakhalire, "Ammutu, amalingaliro-apamwamba," anthu otchuka. Mundikhululukire zimenezo, koma inu mukudziwa chimene ife timachitcha akuluakulu, katchulidwe ka pa msewu tsopano. Ife tonse tikuzidziwa zimenezo mwabwinoko kuti tizinene izo monga chomwecho. "Ammutu, amalingaliro apamwamba, okonda zosangalatsa koposa kukonda Mulungu."

115 Ine ndinaima pamenepo dzulo, ndinayang'ana pa dziwe losambiramo lija pamusi pathu pomwe. Ndipo, ine ndinadabwa, pamene munthu, amene ali mphunzitsi wa Sande sukulu, ananena kwa ine, "Zimenezo sizimayenera kukhala mu Baibulo, pamene Yesu analavula." Anati, "Ndi zotsutsana ndi malamulo aukhondo pamene Yesu analavula ndi kupanga, anadzatenga malovu Ake."

116 Iye anali atayima, akuyankhula, Chigriki chapachiyambi chinati "Iye analavulira pansi." Akuyankhula kwa munthu uyu, ndipo analavulira pansi. Pamene Iye anatsiriza, Iye anatenga dzanja Lake, nafikira pansi, anatenga malovu ndi dothilo nampaka m'maso mwake, ndipo anapaka izo pa maso ake, ndipo anati, "Pita, ukasukusule mu dziwe la Siloam (anatumidwa) ndipo maso ako akatseguka." Ndipo iye anapita ndipo anakasukusula, maso ake anatseguka.

117 Kotero munthu uyu anati kwa ine, "Zimenezo sizingagwire ntchito lero. Izo ndi zotsutsana ndi malamulo aukhondo, malamulo azaumoyo." Ndiyeno munthu yemweyo anatengera banja lake, mkazi ndi ana onsewo kumusi uko ku dziwe losambiramo kumene akazi onsewo ndi amuna, ndipo m'madzi amenewo pa nthawi ya mwezi imene iwo samayenera kuti azilowamo, ndi zonsezo. Iwo samapita konse mu zimbuzi nthawizina, ndi—ndi matupi onse auve amenewo ndi nyansi mmenemo, ndipo iwo akuwalavulira iwo pakamwa pawo, ndi mmaso, ndi zinthu monga chomwecho. Ndiye kenako nkumanena kuti Yesu akulavulira pansi ndi kumupangitsa munthuyo kuti apenye!

118 Ine ndinamubweretsa mnyamata wamng'ono kuchokera kumeneko tsiku lina, iye anati, "Ine ndinameza ena a madzi amenewo," anati, "Ine ndikudwala ngati kavalo. Ine—ine ndikupita kwathu." Mnyamata wamng'onoyo akhoza kukhala ali pano tsopano, yemwe amakhala mu ngolo pafupifupi nyumba ziwiri kapena zitatu kumusi kwa msewu, kumene ine ndinamutenga iye, anati, "Ine sindidzapita konse mmenemo kenanso."

119 Komabe zimenezo zimatchedwa "chitukuko chamakono." Mukuona kumene inu mwafika? Maneno akale akuti "kukhazikika pa zinthu zazing'ono ndi kusiya zazikulu," mwaona. Ine ndikungofunitsitsa ntakumana naye iye tsopano.

Tsopano, ndi zimenezotu. Kulibwino muchoke ku zinthu zimenezo, mwaona.

120 Aluntha, "ammutu, amalingaliro apamwamba, okonda zosangalatsa kuposa kumukonda Mulungu." Ine ndikubwereza Lemba. Mzimu Woyera ukuyankhula momveka kuti izi zikanadzachitika pa nthawi yotsiriza. "Ammutu, amalingaliro apamwamba, okhala ndi mawonekedwe aumulu-. . ." Chabwino, choyamba, "Iwo akanadzakhala osakhutitsidwa, ndi onyoza iwo amene akulondola," odana ndi iwo amene amawakhulupirira Mawu. Mukuwaona iwo? Iwo samagwirizana ndi tizikhulupiriro ta miyambo iti ndi zinthu, kotero iwo amawada iwo.

121 Monga Afarisi aja ndi Asaduki, iwo ankamuda Yesu. Chifukwa chiyani? Chifukwa Iye anali—Iye ankatsutsana ndi kachikhulupiriro kawo. Mukuona? Osati kuti Iye ankafuna kukhala wosiyana, koma, Iye akuyenera kukhala moyo, Iye anali Mawu, Mawu amoyo akukhala moyo. Iye anati, "Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine ayi." Mukuona?

122 Chabwino, chinthu chomwecho chiripo lero. Ngati munthu alalikira zinthu izi, ndipo izo nkusachitika, ndiye ndi zolakwika, chifukwa Lemba linati izo zikanadzachitika. Ndiye ngati izo zichitika, ndiye kuti izo nzolondola; osati kuti munthuyo akulondola, koma Mawuwo ndi olondola. Tsopano, koma ichi ndi chikhalidwe chimene ife tafikamo lero. Inu mwaona, abwenzi, izo ndi zomveka basi. Inu mukuona zimenezo? Ine ndikumanga pamwamba apa kuti ndikuwonetseni inu chimake chake apa pa uvangeri wa m'nthawi yotsiriza.

123 Tsopano zindikirani mu nthawi izi, m'badwo waluntha, "Ammutu, amalingaliro apamwamba, okonda zosangalatsa koposa kukonda Mulungu," kumakhala kunyumba Lachitatu usiku kuti awonere ena a masewero otukwana, "Ife timamukonda Susie," kapena "Lucy," kapena chimene zinthu zonsezo ziri, mkazi kukwatiwa ka thwelovu ndi kumakhala ndi mwamuna, ndipo onsewo amoyo. . .Ndipo, oh, mai, mmodzi aliyense wa iwo anakwatira ndipo anasudzulidwa, ndi kukwatira ndi kusudzula, ndipo inu mumawapanga iwo kukhala mafano, ngati milungu. Koma inu mumakonda kumakhala ndi kumawonera zimenezo kuposa kukakhala pa msonkhano wa mapemphero. "Okonda zosangalatsa kuposa kumukonda Mulungu." Masewera a mpira angobwera m'tawuni, kapena Macolonel ndi Zimphona, kapena aliwonse amene angapezeke akukakumana kuno kwinakwake, iwo amatseka matchalitchi kuti akakhale nawo kumeneko. Mulole Elvis Presley abwere kuno pa msewu, ndi gitala yake, ndi kumakaizungulitsa iyo mmbuyo ndi mtsogolo, kapena ena a anyamata amenewo, Lachitatu usiku, misonkhano ya pemphero itsekedwa. "Okonda zosangalatsa koposa kukonda Mulungu. Ammutu, amalingaliro

apamwamba, osakhutitsidwa, owopsya, ndi onyoza iwo amene ali abwino. Okhala ndi mawonekedwe aumulungu!"

Inu mukuti, "Iwo ndi Achikominisi." Ayi, iwo siali.

124 Iwo ndi mamembala a mpingo, okhala nawo mawonekedwe aumulungu. Koma chiyani? Kumakana Mphamvu yakeyo! Okhala nawo mawonekedwe a Mulungu, koma kumati, "Mulungu samachita zinthu zimenezi. Mwaona, palibe Mphamvu kwa izo, inu mungovomereza ndi kuchita *ichi*, *icho*." Mwaona, palibe kusintha kwa moyo, palibe kalikonse, ndi basi—kungokhala wa mpingo.

125 "Okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kumakana Mphamvu yakeyo. Kwa oterowo chokaniko," Baibulo linatero. "Pakuti uwu ndi mtundu umene umapita nyumba ndi nyumba, ndi kumawatsogolera akazi opusa olemedwa ndi machimo, otsogozedwa ndi zilakolako zosiyanasiyana." Ndizo ndendende zimene Baibulo linanena. Tsopano ife tikukhala mu m'badwo umenewo ndendende. "Koma iwe uzichita ntchito ya mvangeri, upange chitsimikiziro chathunthu cha utumiki wako." Mwaona, ndi zimenezotu.

126 Tsopano, mwa atumiki awa ndi mboni zomwe ife tikuziwona, ife tikupeza mtundu wa mbewu umene ife tirimo. Taonani mtundu wa mbewu yomwe inu mulimo mmawa uno. Taonani mbewu yomwe ife tirimo. Bwanji, Iye anati, kumbali *iyi*, zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akukhulupirira, iwo adzanenedwa ndi kunyozedwa monga masiku a Nowa. Ndipo *apa* padzabwera gulu lina ili kumbuyo kuno likuwaseleula iwo, ammutu, amalingaliro apamwamba, ndi okhala nawo mawonekedwe aumulungu, ndi kumakana chinthu chomwecho chimene inu mukudzinenera. Kotero inu mukhoza—inu mukhoza kuwona mtundu wa mbewu imene inu mulimo, mwaona, atumiki owona awa a lero! Yesu ananeneratu kuti *ameneyo* akanadzakhala ali Satana ndi uthenga wake. Ndipo mtumiki Wake akanadzakhala ali ndi *ichi* chikuchitika, zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Mwaona, atumiki a Satana azidzakhala ndi mawonekedwe aumulungu. Atumiki Ake azidzakhala ndi zizindikiro izi, akutola njoka, kumwa zinthu zakupha, kutululutsa ziwanda, kuyika manja pa odwala, kulandira ubatizo wa Mzimu Woyera, zizindikiro ndi zodabwitsa. Tsopano, ife tiri mu imodzi za mbewuzo, ndipo ife tiri kumapeto a nthawi. Oh, mai!

127 Nzosadabwitsa kuti Yesaya mneneri anati, "Thupi lonse lavunda ndipo ladzaza ndi zilonda, chirichonse." Kodi ife tingapite kuti? Kodi ife tingachite chiyani ngati ife tonse tingasonkhane pamodzi? Izo zingapangitse ilo kuyipa kuposa kale, mwaona, pakanakhala mitundu yonse ya zinthu. Monga iwo akuyesetsa—Bungwe la Mipingo Ya Dziko lonse, izo sizidzagwira ntchito nkomwe, iwo ali ndi

achikunja, osakhulupirira. “Ndipo zingatheke bwanji—awiri angayende bwanji limodzi,” linatero Baibulo, “pokhapokha ngati iwo atagwirizana?” Mukuona? Ndipo palibe awiri a iwo adzagwirizane pamodzi.

128 Chipulumutso ndi chokuchitikira pawekha pakati, osati mpingo, koma pakati pa munthu aliyense payekha ndi Mulungu. Kumayenda ndi Mawu! Inde. Taonani, m’bale, pamene ife tikuwona. Ndipo ine ndikudziwa kuti ndikuchedwa kwambiri.

129 Zindikirani, chizindikiro chofiira chachikulu chothwanima cha Kudza Kwake chatsika. Ife tikudziwa zimenezo. Ine ndikhoza kungotenga Malemba ambiri apa amene ine ndinawalemba kuti ndikusonyezeni inu, chimene, ife tikudzakhala pa nthawi yotsiriza. Ayuda abwerera ku Palestina, mtengo wa mkuyu waphuka masamba ake. Mitima ya amuna ikulephera ndi mantha. Azimayi, chipwirikiti chimene iwo alimo, momwe ine ndingakhoze kubwerera mu Chivumbulutso ndi kukakuwonetsani inu kuti fuko ili pano laikidwa chizindikiro ndi akazi, chiwerengero cha mkazi, nambala sartini. Ife tikuyenera, kuyambira, zigawo sartini, milozo sartini, sartini chirichonse, maiko sartini, chirichonse, sartini, nyenyezi sartini pa dola, chirichonse ndi sartini ndipo mkazi.

130 Pamene ine ndinayima osati kale kwambiri mu Switzerland, ndipo ine ndinali ndikuyankhula. Mkazi anati, “Ine, ife tikufuna kuti tibwere ku Amerika kuti tikakhoze kukhala ndi ufulu monga akazi akumeneko.” Ine ndinawauza iwo zimene anachita. “Ayi,” iwo anati, “ife sitikufuna zimenezo, ndiye.” Mukuona? Mukuona?

131 Koma ndi Amerika. Ife tikhoza kubwerera mmbuyo ndi kukasonyeza zimenezo pomwe pano, kuti zimenezo zikuyenera kukhala mu fuko lino limene likuwuka kumene kulibe madzi, kulibeko anthu. Likuwuka ngati mwanawankhosa, ali ndi nyanga ziwiri zazing’ono, mphamvu ya boma ndi yachipembedzo, koma iwo akulumikizana pamodzi kudzera mu mphamvu zandale, Purezidenti watsopano yemwe ife tiri naye, akubweretsamo Roma kachiwiri.

132 Ine ndikufuna aliyense andiuze ine, wafioloje aliyense pano kapena kwina kulikonseko, pamene Baibulo linalosera kuti Chikominisi chidzalamulira dziko lapansi. Inu musamawope Chikominisi, palibe kanthu kwa icho. Ndi chinthu chonyengezera chimene Mulungu akuchigwiritsa ntchito kuti alange nacho mafuko, kudzalanga fukoli. Zedi. Baibulo limati Roma adzalamulira dziko lapansi. Tayang’anani pa Mfumu Nebukadinezara, loto lake, masomphenya ake, kutanthauzira kwa Daniele, momwe uliwonse wa maufumu amenewo ndi nyengo zinakwaniritsidwira mwangwiro basi, ndipo mpakana kumapeto uko kunali Roma. Kotero, iye adzakhala Roma. Icho

sichidzakhala Chikominisi, iwo ndi basi—iwo ndi zithunzi chabe. Ndizo zonse. Iwo sadzapita nkomwe kulikonse. Ayi, iwo sadzatero.

133 Monga Joseph anangoti, "Mtima wa Africa, achikunja osauka amenewo kumbuyo uko si oti azilamulidwa. Iwo analamuliridwa kale." Ndiro limene liri vuto ndi iwo lero, iwo alamuliridwa kale. Iwo akufuna chikondi, iwo akufuna Mulungu. Ndipo pamene Chikominisi chiri chopanda umulungu, ndiye iwo sadzavomereza konse zimenezo. Ndithudi ayi, ndithudi ayi.

134 Kuwala kofiira kukuthwanima. Chizindikiro chiri pansi. Kudza kwake kwayandikira. Oh, mai! Yesaya, mutu wa 60 ndi ndime ya 2, anati, "Mdima udzaphimba dziko lapansi, ndipo mdima waukulu udzawaphimba anthu." Ndipo ndiko kulondola ndendende.

135 Wamthenga wa m'nthawi yotsiriza ndi Uthenga akuyenera kuti adzakomane ndi zikhalidwe za mnthawi-yotsiriza. Kodi inu simukuganiza chomwecho? Uthenga uwu sukanalalikidwa zaka forte zapitazo. Ayi, Uthenga wa m'nthawi yotsiriza ndi wamthenga zikuyenera kuti zikumane. Kumbuyo uko mmasiku amenewo iwo anali, iwo mwinamwake sibwenzi utagwira ntchito. Koma iwo ukuyenera kugwirizana ndi zikhalidwe za mu nthawi yotsiriza. Kutembenuka, kukhulupirira zizindikiro za Uthenga! Ndiwo Uthenga wa lero. Tsukani miyoyo yanu mu Magazi a Mwanawankhosa ndipo mukhulupirire Uthenga, kuti zizindikiro za nthawi-yotsiriza ziri pano, mbewu ya Uthenga yakhala ikuchitika.

136 Iwo akuyankhula zochuluka kwambiri za kukonzanso, ine ndipita ndi iwo pa zimenezo, monga kukonzanso kwa uvangeri. *Kukonzanso* kumatanthauza "kutsukidwa." Kotero ine ndikuganiza kuti ife tikusowa mulu wa kutsukidwa, ku kusakhulupirira kwathu, ndi kukhulupirira Uthenga. Uko nkulondola. Zochuluka kwambiri za zokayikitsa zathu ndi zodabwitsa. Kukonzanso! Ngakhale mawu achizolowezi mu kumasulira kwa Chigriki omwe amati *kulapa,* amatanthauza "kukonzanso." Ndipo *kukonzanso* kumatanthauza "kutsuka," zakale zonse, zammbuyo, ndi kukhulupirira Uthenga mu mphamvu Yake ndi mawonetseredwe. "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo."

Iwo amati, "Basi kwa m'badwo umenewo."

137 Iye anati, "Mpaka kumapeto a dziko lapansi." Tsopano, winawake akulondola. Ngati munthu amene ali wosakhulupirira ananena kuti izo zinali za atumwi okha, ndipo Yesu Mwiniwake anati "mpaka kumapeto a dziko lapansi," ndiye ine ndimatenga Mawu Ake pa izo. Ndiko, Uko nkulondola!

138 Mulungu akufuna anthu Ake kuti alekanitsidwe ndi kusakhulupirira ndi osakhulupirira. Ambiri a anthu inu

mumapanga kulakwitsa mu izi, nthawizina mumawalola ana anu kuti azikasewera ndi Oswald wamng'ono. Mukuona? Ine sindikutanthauza kuti ndikhale wotsutsa tsopano, ndi wokhuthala, ndi zina zotero, ndi kukhala mtundu wina wa wotentheka. Ine sindikutanthauza zimenezo. Koma inu mumamulola a . . . Inu muzikhala otsimikiza za amene mwana wanu wamkazi akupita naye nthawi yausiku. Mukuona? Mwinamwake inu munamulera iye monga mtsikana wamng'ono waumulungu pafupi ndi tchalitchi, ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa iye amapita kunja ndi Oswald kapena ena a iwo, ndipo—ndipo iye ndi wachikunja, wosakhulupirira, ndipo moyo wake udzafika powonongeka ndipo inu simudzadziwa chimene iye ali. Inu mukuona? Kenako iye adzamukwatira iye, ndipo taonani kumene ana anu ali, zidzukulu zanu, ndiye, inu mwaona. Khalani osamalitsa. Mulungu akufuna kuti anthu Ake akhale olekanitsidwa.

139 Inu mudzawerenge Eksodo 34:12 nthawiyina, ndipo mudzawone chimene Mulungu anamuuza Israeli. "Pamene mukupita mdziko limenelo, mukayeretse chirichonse chimene chiri kumeneko. Musakakhale ndi chinthu chimodzi chochita ndi izo." Yoswa nayenso, mutu wa 23 ndi ndime ya 12, penyani chimene Yoswa ananena, "Tsopano Mulungu wakubweretsani inu ku dziko labwino ili," chimodzimodzi ndi Mpingo tsopano, "ndipo wakubweretsani inu ku dziko labwino ili. Kodi inu mukusangalala nalo?"

Iwo anati, "Ameni, ife tikusangalala nalo."

140 Anati, "Tsopano pali wotsalira wina, osakhulupirira awa kunja kuno, ndipo osati muzikayanjana nawo iwo. Osati muzikayenda nawo iwo." Inu musakatero, mlongo, ngati mnyamata ameneyo akufuna kuti akutengereni inu ku bala kwinakwake, kuti mukangokhala ndi chakumwa pang'ono mwaubwenzi, mukakhale naye kutali! Ndipo chinthu chomwecho, anyamata inu, kwa mtsikana ameneyo amene angachite chinthu chomwecho. Mukakhale kutali ndi iwo!

141 Tsopano inu munena kuti, "M'bale Branham ndi chidempete chachikale." Koma limodzi la masiku awa inu mudzapeza. Inu mukanakhala mu njira imene ine ndinakhalamo, inu mukana—inu mukanadziwa kuti izo nzoona. Inde, bwana.

142 Ndi kangati komwe ine ndawonapo, mu zipinda zolapira, kumene atsikana aang'ono amakhoza kubwera—mwamanyazi. Chipsyera chimenecho chidzapita ndi iye mpaka iye atadzafa, ndi zinthu zimene iye ananena: Nthawi ina analeredwa mu banja labwino la Chikhristu, koma ichi ndi chimene chinachitika, iye anakayenda ndi mnyamata uyu. Mwamunayo anangokhala wokongola kwambiri basi iye sakanakhoza kukhala kutali ndi iye, ndi—ndi zonse monga chonchi. Ndipo, chinthu choyambirira, iye amasuta ndudu ndipo anali ndi botolo

mthumba mwake, ndipo iwo anayamba kumwa, ndipo ndi inu apa. Mukuona? Ndipo ndi uyo apo mwamanyazi ndi izo. Oh, ndi chinthu chomvetsa chisoni. Inu mukuziwona izo ku mbali ziwiri zonse. Chotero ingokhalani kutali, mudzilekanitse nokha! Muzikhala wabwino ndi wachifundo kwa aliyense, koma musakhale ogawana nawo tchimo lawo. Muzikhala kutali ndi ilo. Inde, bwana.

143 Ndipo ndizo nthawizonse, abwenzi, atsogoleri, nthawi iliyonse kudutsa mu kusintha kwa nyengo izi, zakhala zikuwapangitsa anthu kusokonezeka. Sikuti anali anthuwo mochuluka kwambiri, ngati Uthenga ukanakhala uli pa guwa pamene Iwo uyenera kumakhala!

144 Monga ine ndimayankhula ku Bethany College uko, Achilutera. Iye anati, "M'bale Branham, kodi inu mukuganiza kuti ife tiri ndi chiyani?" Ndipo ine . . . iye anati . . .

Ine ndinati, "Chabwino, ichi ndi chimene icho chiri."

145 Iye anati, "Kusiyana kwake ndi kotani pakati pa pentekoste iyi imene inu mukuyikamba ndi ife Achilutera?"

146 Ine ndinati, "Mpingo wa Chipentekoste ndi mpingo wotukuka wa Chilutera. Ndiko kulondola ndendende. Ngati inu mukanakhala pamene inu mumayenera kukhala, inu mukanakhala a Chipentekoste nanunso."

147 Ndipo ife tonse tikuyankhula zokhudza monga ine ndinamumvera winawake akunena mmawa uno, kuti "Mipingo yonse, chonse—chipembedzo choyamba chonse, Akhristu onse anabwera kwenikweni kuchokera ku Roma." Ine ndikufuna kuti winawake atsimikizire zimenezo kwa ine. Ine ndivomereza kuti zipembedzo zonse zinachokera ku Roma. Koma Akhristu anayambira ku Yerusalemu.

148 Kotero ngati utsogoleri wa Chikatolika ukufuna kuti ife tonse tibwerere kwa mayi wa Chikhristu, ine ndigwirizana naye iye kuti, tiyeni tibwerere ku Pentekoste ndipo tonse tikawupeze Mzimu Woyera. Ine ndigwirizana ndi iye pa zimenezo. Kuti, izo sizinabwere konse kuchokera ku Roma, Izo zinachokera ku Pentekoste. Mpingo sunatsegulidwe ku Roma, iwo unatsegulidwa pa Tsiku la Pentekoste. Ndithudi, osati pansi pa mbalume zawo, koma pansi pa ubatizo wa Mzimu Woyera. Icho ndi chimene ine ndikuyesetsa kuti ndinene. Ngati ife tingabwerere mmbuyo, tiyeni tibwerere ku chiyambi cha izo; osati kubwerera ku chipembedzo, inu mupite ku Roma, chifukwa iwo anali oyamba amene anali nalo bungwe kapena chipembedzo, ndipo ndi mayi wa onse a iwo.

149 Ndipo Baibulo linanena chomwecho, mu Chivumbulutso 17, "Iye ndi hule, iyemwini, ndi mayi wa timahule, ana ake aakazi." Mukuona? Icho ndi chimene Baibulo linanena. Yesu Khristu ananena kuti, "Mpingo wa Roma Katolika uja unali hule, ndipo ana ake onse aakazi Achiprotestanti anali timahule

limodzi ndi iwo." Ndipo Iye anati, "Tulukani pakati pawo, anthu Anga, kuti inu musakhale ogawana nawo machimo ake; ndipo Ine ndidzakulandirani inu, ndipo inu mudzakhala ana aamuna ndi aakazi kwa Ine." Mukuona? Kotero ndi zimenezotu, mwaona, "Okhala ndi mawonekedwe aumulungu, ndi kumakana Mphamvu yakeyo," ndi zina zotero.

150 Inu Amethodisti ofunika, momwe inu munkakhalira ndi mphamvu ya Mulungu pakati panu. Ine ndinapita ndipo ndinakaima. . . Ine ndinavala mkanjo wa John pamene ine ndinali mu London, England, kuti ndikamupempherere Mfumu George nthawi imeneyo. Ndipo iwo ananditengera ine kumtunda uko ku Kachisi wa Wesley kumene iye ankalalikira kwa anthu fifitini handiredi mmawa uliwonse faivi koloko, amuna asanapite kukagwira ntchito. Ndinakhala pamenepo pampando pomwe anatembenuza womenyetsa atambala uyu, ndipo ine—ine ndinakhala pampandopo. Ndipo ndinaima pamenepo, ndipo ndinakwera kupita pa guwa lake. Ndipo ndinakapemphera mchipinda chimene iye anapitira Kumwamba. Ine ndinaganiza, "Oh, ngati John akanadziwa chimene mpingo wa Methodisti uwo wachita, iye akanatuluka mmanda ake." Pamene inu munkakonda kupempherera odwala ndi kumakhala ndi zizindikiro zazikulu! Pamene John Wesley. . . atayima kunja uko, kachisi uja ine ndinayima pafupi ndi iye, kumene kuli mtengo. Tsiku limenelo, akulalikira machiritso Auzimu, ndipo a—mpingo wapamwamba wa England, mpingo wa Anglican, unapita ndipo unatembenuka. . . Gulu la mamembala amenewo linabwera kumeneko ndipo linamasula nkhandwe ndi gulu la agalu, ndipo linabalalitsa osonkhana a John. John wokalamba wamng'ono sanalemerepo konse mapaundi handirede ndi teni nthawi iliyonse m'moyo wake, koma iye anatembenuka ndipo analoza ndi zala zake, ndipo iye anati, "Iwe wachinyengo! Dzuwa sililowa pa mutu wako katatu mpaka iwe utandiitana ine kuti ndidzakupempherere iwe." Ndipo iye anafa madzulo amenewo, ali ndi zopweteka mthupi lake, akumuyitana John kuti abwere adzamupempherere iye. Ndipo iye anafa. Mukuona? Oh, ngati inu Amethodisti mukanakhala Amethodisti monga choncho, inu mukanakhala muli Achipentekoste. Uko nkulondola.

151 Nanga bwanji inu Abaptisti? Inu mumathamangira ku tchalitchi kwa maminiti pang'ono, ndipo abusa akalalikira kupitirira maminiti fifitini inu mumafuna kuwachotsa iwo. John Smith, woyambitsa wa mpingo wa Baptisti, ankapemphera usiku wonse pa nthawi, ndipo ankalira chifukwa cha machimo a anthu mpaka maso ake ankatsekeka chifukwa cholira, ndipo mkazi wake ankakhoza kumutsogolera iye ku tebulo ndi kumudyetsa iye kuchokera mu supuni, kadzutsa wake. Simungathe kupemphera maminiti fifitini panonso. Chavuta ndi chiyani? Mwaona, inu mwazisakaniza Izo ndi miyambo.

152 Uthenga ukupitirirabe. Israeli ankatsatira Lawi la Moto. Pamene Ilo layima, iwo ankayima. Kumene Ilo linkapita, iwo ankapita. Lawi la Moto likusunthirabe chitsogolo. Inde.

153 Tsopano ife tikupeza kuti ndi atsogoleri amene amachita zimenezo. Atsogoleri nthawizonse akhala ali osakanizika. Tayang'anani pa Datani wakale kumbuyo uko mu nthawi ya Baibulo, mu nyengo ya Mose ya chilamulo. Iye anali amene anatsogolera gulu losakanizikana, Datani, anali Korah; pamene Mulungu anadzutsa mneneri Wake Mose, ndipo iye anali ndi Mawu a Ambuye. Iye anali ndi anthu thuu millioni ndi theka kunja uko mu chipululu, ndipo Yatero anadzabwerapo ndipo anadzati, "Mose, izi zikupha iwe, kupsyinjika kwako ndi kwakukulu zedi." Mulungu anatenga gawo la Mzimu Wake ndipo anawuyika Iwo pa akulu sevente, ndipo iwo analosera. Izo sizinamufooketse Mose mpang'ono pomwe. Iye, koma Mose anali akadali yankho lotsiriza, chifukwa iye anali ndi PAKUTI ATERO AMBUYE.

154 Inu simungapite pansi pa gulu la anthu. Ine—ine ndimatsutsa nthawi iliyonse imene—imene inakhalapo, pamene Mulungu anayamba wagwiritsapo ntchito gulu la anthu. Iye amamugwiritsa ntchito munthu mmodzi. Ndendende. Munthu mmodzi pa nthawi, chifukwa anthu awiri amakhala ndi malingaliro awiri. Munthu mmodzi! Kulondola ndendende. Zindikirani tsopano, nyengo iliyonse zakhala ziri mwanjira imeneyo, njira yonse kudutsa, izo zakhala ziri mwanjira imeneyo nthawi iliyonse.

155 Ndipo apo panayima Mose. Ndipo kodi inu mukudziwa chimene Korah ananena? Iye anati, "Bwanji, Mose akuchita ngati iye ndi yekhayo amene angalalikire, iye ndi mmodzi yekhayo amene ali ndi Uthenga. Oh, ife tikudziwa kuti Lawi la Moto lija limapachikika pa iye, ife tikudziwa kuti Kuwala kuja kuli pa iye, ife tikudziwa zonsezo, koma iye akuchita ngati iye ndi mmodzi yekhayo amene ali ndi Uthenga."

156 Iye sankatanthauza zimenezo. Iye sankatanthauza izo mwanjira imeneyo. Iye ankayesetsa kuti awakonze anthuwo. Alipo malingaliro ochuluka kwambiri. Inu mukuyenera kumvetsera kwa chinachake. Ndipo chinachitika ndi chiyani? Mulungu anati, "Ungodzilekanitsa wekha kwa iye, chifukwa Ine ndimumeza iye ndi osonkhana akewo mnthaka." Ndipo nthaka inatseguka ndipo moto unatuluka, ndipo iwo anapita pansi. Mukuona?

157 Osakanikirana, atsogoleri, atsogoleri ndi amene anayambitsa vuto pakati pa anthu. Ngati izo zikanapanda kutero, lero ife tikanakhoza kubwera kuno mu mzinda uno ndipo mpingo uliwonse ndi osonkhana aliwonse akanabwera pamodzi. Bwanji, iwo akanakhala ndi malo awa, iwo akanakhala, oh, malo ogulitsira mowa aliwonse akanatsekedwa. Bwanji,

mzinda uno ukanakhala wowuma kwambiri mpaka wogulitsa mowa akanayenera kudzikonzekeretsa yekha kwa theka la ora kuti apeze chinyezi chokwanira kuti alavule. Iye... Bwanji, izo zikanakhala chomwecho! Oh, ndikhululukireni ine, ine sindimayenera kuti ndinene zimenezo. Dikirani. Ichi, chimene ine ndikutanthauza ndi ichi, ife tonse tamwazikana. Ndi atsogoleri. Mulungu akhoza kubwera kuti adzachite chinachake, ndipo atsogoleri a magulu aang'ono awa amawopa kuti chinachake chitayika, iwo amakhala...amawachotsa iwo kwa Izo, mmalo movomereza Uthenga wa Mulungu. Anali atsogoleri, mmasiku a Nowa. Anali atsogoleri, mmasiku a Mose. Anali atsogoleri, mmasiku a Yesu. Ndi atsogoleri, lero mu Mzimu Woyera. Unyinji wosakanikirana! Iwo amati, "Oh, aloleni akazi azichita zimenezo. Bwanji inu mukuwakalipira iwo?"

158 Monga ine ndanenera, ine ndikukhulupirira kuno kale, winawake ananena kwa ine tsiku lina, chifukwa ine nthawizonse ndimayesetsa kuwayika alongo anga mu mzere. Mukuona zimenezo, iwo ndi—iwo amakhala chandamale. Iwo akhala ali chandamale mu m'badwo uliwonse. Satana anawagwiritsa iwo ntchito kumbuyo uko mmunda wa Edeni, ndipo iye wakhala akuwagwiritsa ntchito iwo nthawi iliyonse. Ndipo pamene Baibulo lilozera za Amerika ndi akazi ake mmasiku otsiriza, ndiye ine ndimayamba kukhomerera pa zimenezo. Ndipo winawake anati, "M'bale Branham, anthu amakutengani inu ngati mneneri."

Ine ndinati, "Ine sindiri."

159 Iye anati, "Koma iwo amakutengani inu monga choncho. Bwanji inu osamawaphunzitsa anthu amenewo momwe angapezere mphatso zazikulu zauzimu? Kuwaphunzitsa iwo zinthu ngati inu...Mulungu amachita nanu, ife tikudziwa zimenezo." Anati, "Bwanji inu osamawaphunzitsa akazi amenewo mmalo momawadula iwo nthawizonse?"

160 Ine ndinati, "Ine ndalalikira kwa iwo kwa zaka sartewani, ndipo iwo ali...Ine ndingawaphunzitse bwanji iwo, ine ndingawaphunzitse bwanji iwo algebra, pamene iwo sakudziwa nkomwe ma ABC awo? Nchifukwa chiyani iwo samamva ndi kumachita ngati akazi? Nchifukwa chiyani iwo amakhala akuchita momwe iwo akuchitiramu? Iwe ungawaphunzitse bwanji iwo zinthu zauzimu pamene iwo sakukhulupirira nkomwe zinthu zathupi? Iwe ungawaphunzitse bwanji iwo zinthu zimenezo?" Mulole mpingo ubwere mu dera limenelo, ndiye kenako iwo akhoza kuphunzitsidwa mu dera limenelo momwe angalandirire mphatso za Mulungu ndi momwe angawonetsere mphatso ndi zinthu. Koma Mzimu Woyera sudzazilola izo kuti zibwere mpaka mtima umenewo utakhala wolondola ndi wokonzeka kulandira izo.

161 Ndiye, Mulungu akuyima pamenepo ngati mphamvu yaikulu yokanikiza. Musamawope kuti pakhala ochuluka a iwo. Simungathe kumumaliza Mulungu. Kodi inu mungalingalire khoswe wamng'ono pafupifupi wotalika *choncho*, mbewa yaing'ono pansi pa nkhokwe zazikulu za ku Igupto, ikuti, "Ine kulibwino ndizidya njere imodzi ya tirigu pa tsiku, iye akhoza kundithera kukolola kotsatira kusanafike"? Kodi inu mungalingalire nsomba yaying'ono yotalika pafupifupi *chonchi*, ikusambira uko pakati pa nyanja, nkumati, "Ine kulibwino ndizimwa madzi awa motsinira, chifukwa, inu mukudziwa, iwo akhoza kudzawuma nthawiyina"? Oh, mai, ndiko kuyesetsa kumalizitsa ubwino wa Mulungu ndi chifundo kwa anthu Ake! Iye akufuna kukudalitsani inu. Iye wakonzeka, Iye akukanikiza. Kodi inu mungalingalire kutenga madzi onse mdziko lapansi, nyanja ndi chirichonse, ndi kuwaunjika iwo mu paipi imodzi ya mapazi foro ndi kuiyika iyo pamwamba apo? Kupanikizikako kungakhale pansi pake, kuyesetsa kupeza kamng'alu kakang'ono koti atulukirepo. Izo ziri ngati kukanikiza kwa Mzimu Woyera ukuyesetsa kubwera pansi pa moyo uliwonse.

162 Koma iwo sangachite zimenezo, iwo amakonda tizikhulupiriro ndi zinthu kwambiri kuposa momwe iwo amamukondera Mulungu. Iwe ukuyenera kugulitsa zinthu za mdziko, ndi kumukhulupirira Mulungu. Zimenezo sizingakanidwe, inu mwaziona izo chaka ndi chaka, ndipo nthawi ndi nthawi. Ndipo Joseph ananena nthawi ina, "Izo sizimaphonya konse. Izo zikuyenera kukhala Mulungu." Mukuona? Ndipo ndi lonjezo la Mulungu la tsikuli. Osati ine; ine si lonjezo la Mulungu. Ndine munthu. Ine ndikuyankhula za Mzimu Wake Woyera umene uli pano. Ndiro lonjezo la tsikuli, "Paliponse, aliyense."

163 Tsopano, ife tikupeza kuti iwo anali amenewo. Ndipo, taonani, ndipo ife titenge mwachitsanzo, Balamu. Balamu, iye anabwera kumeneko ndipo anadzawaphunzitsa anthu chiphunzitso chake, ndipo iwo anati, "Tsopano taonani, ndife tonse okhulupirira, ndife—ndife ana a ana aakazi a Loti, Moabu kumtunda uko." Anati, "Ife ndife tonse ofanana basi." Ndipo iye anawasakaniza iwo, anayambitsa kumakwatirana. Iye anawapangitsa akazi okongola Achimoabu amenewo, onse kuti aziwoneka modolola, ndipo anabwera kuno ndipo anadzawauza ana aamuna a Mulungu awa kuti iwo anali—iwo anali "onse ofanana, pambuyo pa zonse; Mulungu ndi Mulungu wa mitundu yonse, ndipo chirichonse chiri bwino." Ndipo iye anawakwatitsa iwo limodzi. Ndipo Mulungu anajambula mzere wolekanitsa, ndipo anawapangitsa iwo kusiya nyumba zawo ndi chirichonse. Chinali chiyani icho? Mukuona chinthu chimenecho? Ndendende basi zimene zinachitika kumbuyo uko chisanachitike chigumula, "Pamene ana aamuna a Mulungu anawona ana aakazi a anthu,

iwo anali okongola kuyang'ana pa iwo, ndipo iwo anawasilira iwo ndipo anadzitengera kwa iwo akazi." Mukuona? Chinthu chomwecho chinachitika uko.

164 Ndipo chinthu chomwecho tsopano! Panonso ndi chinthu chomwecho. Inu mukuyenera kuchiwona icho. M'badwo uliwonse umanena zomwe ziti zidzachitike pa wotsatirawo. Ndi izi apa. Ife tikuziwona izo. Ife tikudziwa kuti ndi zomwezo, chifukwa Baibulo apa likunena kuti ndi chimodzimodzi tsopano monga momwe zimakhalira. Chabwino. Tsopano, ndipo zonsezo zikuwerengedwa, ndithudi, kwa a—tsiku limene ife tikukhalamo.

165 Tsopano, a—kuitana kwa tsikuli, zonse zimene zikuwerengeredwa pakati pa mipingo lero, ndi mamembala. Ndizo zonse zimene iwo akufuna ndi mamembala. Tsopano, ife tonse tikudziwa mbalume ya Baptisti mu 1944, anati, "Ife tikhala ndi millioni enanso, '44." Ife tikumudziwa M'bale wathu wofunika, wachisomo Billy Graham, ife tikuwawona malo ake mu Lemba, kumene iye amapitako, chimene iye amachita. Koma nthawizonse ndi "zigamulo, zigamulo zochuluka kwambiri zikupangidwa." Chipembedzo chabe, ndizo zonse zimene iwo akuzifuna. Mukuona?

166 Umo ndi momwe zinkachitikira mmasiku a Yesu, chinthu chomwecho. Iwo sanali anthu oyipa. Iwo anali akhungu. Ndizo zonse. Iwo anali akhungu ku Choonadi. Yesu anawauza iwo choncho, anati, "Inu Afarisi akhungu ndi Asaduki, zonse zimene inu mumachita!" Kodi Iye anati inu mumachita chiyani? "Inu alembi, Afarisi, ndinu akhungu!" Iye sanati, "Ndinu ochimwa." Iwo anali ochimwa, koma chimene ife timachitcha tchimo.

167 Tsopano, ife timalitcha tchimo, "Kuchita chigololo, kusuta, kunama, kuba, zinthu monga zimenezo, ndiro tchimo." Zimenezo si tchimo. Zimenezo ndi zotsatira za kusakhulupirira.

168 Baibulo linati, "Iye amene sakhulupirira watsutsidwa kale." Kusakhulupirira mu Mawu, ndi tchimo.

169 Tayang'anani pa amuna amenewo, oyera. Bwanji, inu simukanakhoza kuyika chala pa iwo, mwamakhalidwe. Agogo awo aamuna, ndi agogo a-agogo aamuna, ndi agogo a-agogo a-agogo aamuna, ndipo agogo a-agogo a-agogo a-agogo aamuna onse anali ansembe. Iwo ankasunga lamulo limenelo ndi miyambo ya akulu akulu ndi makolo, mwangwiro basi, kutsika kudutsa mmibadwo. Panalibe chilema chimodzi pa iwo. Ngati iwo akanatero, iwo akanagendedwa. Amuna abwino. Ndipo Yesu anati, "Ndinu a atate wanu mdierekezi!" Chifukwa chiyani? Chifukwa iwo sanauwone Uthenga, Mawu. Iye anali pamenepo.

170 Ndipo iwo anati, "Chabwino, munthu uyu akuyesetsa kuti aphwasule mipingo yathu."

171 Iye anati, "Inu Afarisi akhungu ndi Asaduki!" Iye anati, izi ndi zomwe Iye ananena, Iye anati, "Inu mumaizungulira

nyanja kuti mupange wotembenuka mmodzi. Zonse zomwe mungachitire membala m'modzi! Ndipo pamene inu mumubweretsa iye mu chipembedzo chanu, iye amakhala pawiri mwana wa gehena mochuluka kuposa momwe iye analiri pamene iye anali kunja uko." Ndizo ndendende zomwe Yesu ananena.

172 Ndipo ngati pali chirichonse chimene chiri chosalungama ndi chirichonse chimene chiri chopandaumulungu, ndi kutenga membala wachikale wa mpingo yemwe akuganiza kuti ndi wabwino kwambiri, ndipo iwo osamakhoza kuwona kudzera mu chirichonse koma magalasi awo omwe. Ine sindikutsutsa. Koma, inde, ine ndirinso, nanenso. Ndipo, ndizo ndendende kulondola basi. Ndipo Yesu anati, "Ndinu mwana wa gehena pawiri kuposa momwe inu munali pamene inu munkayamba." Ndipo pamene ife titenga mipingo, kuti ziribe kanthu ndi mamembala angati amene inu muli nawo mu mpingo umenewo, ndi kuwaona iwo akupita ku njuga ndi ku mipikisano ya akavalo, ndi kumaima kunja kuno ndi akazi atavala akabudula, nkumayenda chokwera ndi chotsika mmisewu, ndi kumaimba mu kwaya, ndicho chopunthwitsa chachikulu chimene wochimwa anayamba wakhalapo nacho. Ndendende. Iwo akuwayembekezera anthu amenewo amene amadzitcha okha Akhristu kuti azikhala moyo wabwino, kuti azikhala munthu wosinthika. Ameneyo ndi chitsanzo. Ameneyo ndi chopunthwitsa. Ameneyo ndi wachinyengo. Ndizo kuchulukitsa ka teni woyipa kuposa momwe inu munayamba mwakhalirapo. Inu mukanakhala bwinoko mukanakhala kunja uko monga munkachitira.

173 Apo ndi pamene munthuyo amabwera, nkuti, "Chabwino, iwo samakhala moyo wosiyana ndi umene ine ndimakhala. Chabwino, ndithudi ayi. Ndine, ine ndingakhale wabwino monga iwo aliri." Icho ndi chopunthwitsa. Ndiko kulondola ndendende. Kuwawona iwo akuti, chabwino, wochimwa wina akuyenda ndikuti, "Yesu ananena izi apa."

174 "Ah, izo sizinali, pakuti izo—izo sizikutanthauza zimenezo. Kuti—kuti, Iye sankatanthauza zimenezo apo pomwe. Zimenezo zinali za m'badwo wina." Bwanji iwe wosakhulupirira! Mukuona? Chavuta ndi chiyani? Inu mumayika chopunthwitsa mu njira ya munthu ameneyo.

175 Yesu, kapena ine ndikutanthauza mu Masalimo, Davide anati, "Musakhale pa mpando wa onyoza, musayime m'njira ya opanda umulungu." Mukuona? "Musadziyike nokha mu njira ya opanda umulungu monga chomwecho ndi kukhala mu mpando wa onyoza, kumawaseka iwo amene ali olondola, ndi kumayima pamenepo nkumati iwo anali mawonekedwe aumulungu. Koma iye amene amakondwera mu lamulo la Ambuye, iye amakonda kuchita zimenezo, iye adzakhala monga mtengo umene wabzalidwa m'mphepete mwa mitsinje ya

madzi. Masamba ake sadzafota. Ndipo chirichonse chimene iye achita chidzapambana, izo zidzafika pochitika ndendende basi." Ndiwo mtundu wa mpingo umene Mulungu akuwufuna. Atsogoleri akhungu a akhungu, kumapanga, mmasiku otsiriza ano, onyoza akubwera, ndi zina zotero.

176 Uthenga wa mvangeri wa m'nthawi-yotsiriza ndi wochokera pa Malaki 4. Iwo ndi kubwezeretsa. Uthenga ndi wamthenga, ziwiri zonsezo, zidzayenera kukhala kubwezeretsa kwa Chikhulupiriro. Yuda anatero, mu Bukhu la Yuda, pafupifupi zaka sarte kutachitika kupachikidwa, iye anati, "Abale, ine ndikupereka kulimbika konse kuti ndikulembereni inu za Chikhulupiriro chawamba, kuti inu mukuyenera kulimbanira moonamtima Chikhulupiriro chimene chinaperekedwa kamodzi kwa oyera kumbuyo uko." Mukuona? Mukuona? Malaki ananena, kwa masiku otsiriza, mneneri wotsiriza wa Chipangano Chakale, kuti "Lisanadze Tsiku lalikulu ndi lowopsya la Ambuye, Ine ndidzatumiza kwa inu Eliya mneneri. Ndipo iye adzabwezeretsa Chikhulupiriro cha ana kubwerera, kapena Chikhulupiriro cha ana kubwerera kwa makolo, basi isanafike nthawi ya chiwonongeko." Ndi chiyani chimenecho? Ndi Uthenga umene ukupita, Uthenga ndi wamthenga wa mmasiku otsiriza, zimenezo si kuwabweretsa iwo ku kachikhulupiriro, koma kuwagwedeza iwo kuti achoke ku tizikhulupiriro timeneto ndi kuwabweretsanso iwo ku Chikhulupiriro chapachiyambi cha makolo, makolo achipentekoste, pamene Mpingo uti udzakhale mmasiku otsiriza. Osati makolo a m'nthawi ya Mose, koma makolo achipentekoste.

177 Makolo a m'nthawi ya Mose anali Malaki 3, "Ine ndikutumiza wamthenga Wanga patsogolo pa nkhope Yanga, kuti adzakonze njira pamaso pa Ambuye." Mateyu 11:6 amanena chinthu chomwecho. Yesu akuchitira umboni zimenezo pamene Iye anamuwona Yohane, anati, "Kodi inu munapita uko kukawona chiyani, mwamuna atavala makolala abwino, otembenuzidwa, ndi zina zotero? Osati Yohane." Iye anati, "Iwo amene amavala monga choncho amakhala mu nyumba zachifumu, ndi zipembedzo zazikulu izi, amene amapsyopsyona makanda, ndi kukwatitsa, inu mukudziwa, ndi zina zotero, kukwirira akufa, ndi kukwatitsa achichepere, ndi zina zotero. Iwo ali kumbuyo uko." Anati, "Kodi inu munapita kukawona chiyani? a—bango logwedezeka ndi mphepo iliyonse? Ayi, osati Yohane. Ayi, ayi, iye sanagwedezeke pamene iwo anamuwukira iye."

178 Anati, "Iwe sudzakhala ndi mgwirizano ngati iwe utapite kumeneko." Izo sizinapange kusiyana kulikonse kwa Yohane, iye anapita mulimonse. Mukuona?

179 Anati, "Kodi inu munapita kukawona chiyani, mneneri?" Anati, "Ine ndikuti, ndipotu woposa mneneri! Ndipo ngati inu

mungakhoze kumvetsa izo, uyu ndi yemwe anayankhulidwa ndi mneneri, kuti, 'Ine ndidzatumiza wamthenga Wanga patsogolo pa nkhope Yanga, kuti adzakonze njira,'" Malaki 3.

180 Ndipo mu Malaki 4, kwa m'badwo wa mpingo, Iye anati, "Ine ndidzatumiza kwa inu Eliya lisanadze tsiku limenelo." Tsopano, ameneyo sakanakhoza kukhala Yohane, chifukwa dziko silinawotchedwe kumbuyo uko ndi olungama kuyenda pa mapulusa a oyipa. Ayi. Ndi m'badwo uno, Uthenga umene uti udzapite! Iwo udzachita chiyani? Udzabwezeretsa Chikhulupiriro cha anthu, Mpingo lero umene uli kunja kwa zivundi zosiyanasiyana izi ndi thupi lovunda, lazilonda la chipembedzo, kubwerera ku Chikhulupiriro chamoyo ndi Mulungu wamoyo. Uthenga wakhala ukupitirira kwa zaka. Uko nkulondola. Ino ndi nthawi tsopano yoti ife tilandire ndi kukhulupirira: uvangeri wa m'nthawi-yotsiriza ndi woti ubwezeretse. Yoweli ananena chinthu chomwecho, "Ine ndidzabwezeretsa zaka zonse zomwe chimbalanga chinadya."

181 Taonani apa. Mukukumbukira Uthenga wanga wa posachedwapa wa mtengo wa Mkwatibwi, mwaona, momwe iwo anamutengera Yesu? Iye anali Mtengo, Umodziwo omwe Davide anawuwona, Mtengo wobzalidwa m'mphepete mwa mitsinje ya madzi, chipatso Chake mu nyengo, Mtengo wangwiro kwambiri. Ndipo iwo anamudula Iye ndipo anamupachika Iye pa mtengo wachi Roma wochita kupangidwa ndi munthu, wochitira mnyozo. Koma kodi Iye anachita chiyani? Anawukanso pa tsiku lachitatu. Kodi Iye anachitanso chiyani? Iye anakhazikitsa Mtengo wa Mkwatibwi, mwamuna ndi mkazi monga mitengo yomwe inali mmunda wa Edeni, mitengo iwiri. Umodzi wa iyo, mtengo wa moyo, ndipo winawo mtengo wa imfa. Ndipo kodi Iye anachita chiyani? Iye anabwera kuti adzawombole mtengo uwu. Chotero pokhala kuti Iye anawuwombola iwo, pa Kalvare, Iye ndi wokonzeka kuti amubzale iye tsopano. Oh, mai! Ine ndimayamba kumverera mwachipembedzo pamene inu munena zimenezo, mwaona. Kuti abwezeretse mtengo Wake wa Mkwatibwi, umene umayenera kukhala uli mu Edeni, koma iwo unagwa kumeneko chifukwa sunawakhulupirire Mawu. Koma apa Iye abwezeretsa mtengo umene uti udzakhulupirire Mawu! Ndipo pamene iwo unabwera pa Tsiku la Pentekoste, Chiphunzitso chapachiyambi chija, Chikhulupiriro chapachiyambi chija, ndiye kodi Roma anayamba kuchita chiyani? Anatumiza chirimamine, anatumiza chimbalanga. Ndipo chirichonse chinachotsapo gawo lake pa chipatsocho, masamba ndi chirichonse, ndipo zinayamwa iwo wonse mpaka pansi.

182 Koma kodi mneneriyo anawona chiyani, iye anati, "Koma Ine ndidzabwezeretsa mtengo umenewo, atero Ambuye." Iwo unayambira kumbuyo uko kubwerera mu kukonzanso. Kodi iwo unachita chiyani? Unapanga bungwe. Mulungu anawudula

iwo, mu Yohane Woyera 14, anadula bungwe lonse pa iwo. Ndipo iwo unabwereranso kwa Wesley, iwo anapanga bungwe. Anawudulapo iwo.

183 "Koma Ine ndidzabwezeretsa!" Iwo ukubwerabe. Tsopano kodi izo zikuchita chiyani? Mu nthawi yakumadzulo sikudzakhala bungwe. Kudzakhala a—pamwamba. Kodi chipatso chimacha pati poyambirira? Pamwamba. Bwanji? Dzuwa limachimenya icho. Ndipo mu nthawi yakumadzulo mbewu zabzalidwa tsopano kwa mtengo wa Mkwatibwi wa m'nthawi yakumadzulo. Pamene Mtengo wa Moyo ukubwereranso ku mtengo wa Mkwatibwi. Mukuona? Ndipo Kuwala kwa kumadzulo kwatulukira tsopano kuti kudzathirire ndi kudzakhwimitsa chipatso chimenecho chimene chakhala chiri pa mtengo umene wakhala utabzalidwa. Mbewuzo zafesedwa. Mukuona? Nthawi ya kumadzulo. Kotero uvangeri wa m'nthawi ya kumadzulo udzakhala chilemba cha Malaki 4, kuti udzabwezeretse chikhulupiriro cha anthu kubwerera ku Chikhulupiriro cha makolo. Inde, bwana. Kubwerera ku Miyala yomangira! Ameni. Kubwerera ku . . .

184 Lero atsogoleri kachiwiri akuti, "Manambala, manambala!" Zimene kumbuyo uko iwo ananena mu nthawi ya Yesu, mu nyengo imeneyo. Yesu anati, "Achinyengo inu! Alembi inu, Afarisi inu, mumazungulira nyanja kuti mupange wotembenuka mmodzi, kupeza membala mmodzi, ndipo pamene inu mumubweretsa iye mkati iye amakhala mwana wa gehena kawiri kuposa momwe iye anali pamene iye ankayamba." Ndipo lero iwo—iwo amawononga mabillioni a madola ndi kuchita chirichonse chimene iwo angathe kuchita kuti apeze membala mmodzi wina wa mpingo. Ndipo, pamene inu mutero, iye amakhala woipa kwambiri kuposa momwe iye anali kunja uko. Inu mukhoza kungopanga wachinyengo kuchokera mwa iye, kumawalola amuna kumachita zinthuzo, kutuluka kupita mdziko ndi kumakaseka ndi kumanyoza Uthenga, ndi chirichonse monga chomwecho. Ndizo, onani, atsogoleri a tsiku lino kachiwiri akuti, "Manambala, manambala, manambala!" Izo, ndizo zonse zimene zikuwerengeredwa lero, ndi manambala, zigamulo.

185 Tsopano, amenewo ndi mawu aakulu chotero lero, "zigamulo." Ine ndingakonde winawake atapanga kugamula koti azimutumikira Mulungu mmalo mojowina mpingo. "Pangani chigamulo, lowani, mudzalembe dzina lanu pa bukhu," kutumiza gulu lonse lalikulu la anthu kumusi uko, akalembedwe. "Dzina lako ndi ndani?" "John Jones." "Kodi iwe ukumuvomereza Khristu ngati Mpulumutsi wako?" "Eya." "Iwe ukumukhulupirira Yesu Khristu kukhala Mwana wa Mulungu?" "Eya." Satana amachita chinthu chomwecho, chinthu chomwecho. Baibulo linati iye amatero. Iye amakhulupirira ndipo amanjenjemera. Inde, bwana.

186 Koma iwe sumanjenjemera pamene ukukhulupirira kwenikweni, iwe umasangalala, ameni: "Onse amene amakonda kuwonekera Kwake." Monga ine ndinanenera winawake mosalekeza akumandiuza ine, kunditumizira ine makalata, "M'bale Branham, inu mumawawopsyeza anthu pafupi kuti amwalire, pomawauza iwo kuti nthawi yotsiriza ikubwera." Kuwuwopsyeza Mpingo? Mai, ndicho chinthu chaulemelero kwambiri chimene chingachitike, Kudza kwa Ambuye, nthawi yotsiriza. Ine ndikanakonda iyo ikanakhala pakali pano. Ndithudi. Chabwino, ndicho chinthu chaulemelero kwambiri chimene ine ndinayamba ndachiganizirapo, kuti ndikumane ndi Ambuye wanga. Mkanjo wakale uwu wa mnofu ine ndidzawugwetsa, ndipo ndidzawuka ndi kukalandira mphotho yosatha, kudzabwereranso ku unyamata kachiwiri, ndi kudzakhala ndi Ambuye wanga kwanthawizonse, limodzi ndi anthu anga onse. Bwanji, mai! Ine sindingakhoze kuganiza za kuvutika kudutsa mu tchimo ili ndi yesero, ndi zowawa ndi maululu mu nyumba ya tizirombo yakale iyi kuno. Kuchisiya chinthu ichi ndi kupita ku—korona wa chirungamo, bwanji, ndi chinthu chaulemelero kwambiri chimene ine ndinayamba ndachimvapo! Monga Mtumwi Paulo anati, "Ine ndamenya nkhondo yabwino, ine ndamaliza ntchito yanga, ine ndasunga chikhulupiriro changa, kuyambira pano pali a . . . Ndasunga Chikhulupiriro, ndipo kuyambira tsopano pali korona wachirungamo wosungidwira kwa ine, amene Ambuye wolungama ati adzandipatse ine mu tsiku limenelo; osati ine ndekha, koma onse amene amakonda kuwonekera Kwake." Osati *kukhulupirira* kuwonekera Kwake; koma "kukonda" kuwonekera Kwake, chisangalalo choterocho kudziwa kuti Iye akubwera! Ndithudi! Inde, bwana!

187 Koma lero ndi "mamembala," ndi "zigamulo," ndi "muzibweretsa mamembala a mpingo," mamembala ambiri. Ndicho chimene . . . Umenewo si uvangeri wa m'nthawi yakumadzulo.

188 Tsopano ine ndiyima kwa miniti yokha, ndipo ine ndikungofuna kuti ndiyankhule nanu kuchokera mu mtima mwanga. Ndikudalira kuti sindinatero—sindinakusungeni motalika kwambiri. Ndi . . . Ine ndiri nawo pafupifupi maminiti seveni, eyiti panobe, ndipo ine ndikungofuna kuti ndiyankhule nanu kuchokera mu mtima mwanga.

189 Kodi si choonadi chimenecho tsopano, "Zigamulo, zajowineni tchalitchi. Inu muwusiye mpingo wa Methodisti ndipo mubwere mudzatijowine ife, a Baptisti. Kapena, inu muwasiye a Baptisti ndipo mubwere mudzatijowine ife, a Methodisti, Presbateria, Lutheran"? Katolika akutenga onse, mwaona. "Membala, membala, membala, membala, zigamulo, zigamulo."

190 Kodi miyalayo ndi yaubwino wanji ngati mulibe mmisiri

wa miyala kuti ayiseme iyo? Kuvomereza ndi miyala. Pamene Petro anapanga kuvomereza kwake, Yesu anati, "Iwe ndiwe Petro, mwala wawung'ono." Koma kodi mwalawo uli ndi phindu lanji ngati palibe mmisiri wa miyala pamenepo woti awuwumbe iwo kukhala mwana wa Mulungu? Inu mukungowunjika mulu wa miyala. Nkulondola uko? Izo sizikuchita ubwino mpang'ono pomwe. Mukuona? Madzi amaperepesa mwala. Mwaona, uko nkulondola, amenewo ndi anthu. Ndi yaubwino wanji miyala ngati inu mulibe mmisiri woona wamiyala ali ndi chida chabwino chakuthwa kuti amuwumbe iye kuti akhale pamalo oyenera m'Nyumba ya Mulungu? Ndikungofuna kuti ndikufunseni inu, ndi zaubwino wanji zigamulozo, ndi zaubwino wanji kuyika dzina lanu m'bukhu? Ndi zaubwino wanji kubwera kudzajowina mpingo, ngati mmisiri wamiyalayo sali kumeneko amene angawuseme iwo ndi kuwapanga iwo kusiya *ichi* ndi *icho,* ndi kuwadula iwo ndi kuwapanga iwo mwanjira Iyi, ndi kuwalinganiza iwo ndi kuwapanga iwo monga Akhristu omwe akukhala mu Nyumba ya Mulungu, ndi zizindikiro zikuwatsatira okhulupirira?

191 Umenewo ndiye uvangeri wa m'nthawi yotsiriza, kutenga miyalayo ndi kuyiwumba iyo. Mukuona?

192 Kodi miyalayo ingakhale yaubwino wanji ngati mutangoiwunjika? Isiyeni iyo izikhala kumene iliko, zingachite bwinoko pang'ono kukhala kunja uko kuposa kudzaiwunjika iyo pamodzi. Iyo ikhoza kufunidwa kunja uko, ndipo palibe umodzi wa iyo kunja uko. Mwaona, uko nkulondola. Mwala sungakhale ndi ubwino popanda mmisiri wamiyala.

193 Yesu amawerengera khalidwe, osati mamembala. Inu mukudziwa zimenezo? Iye amawerengera makhalidwe. Mulungu nthawizonse wakhala akuyesetsa kuti amutenge munthu mmodzi mdzanja Lake. Ndizo zonse zimene Iye akusowa, ndi munthu mmodzi, ndipo Iye adzachita ntchito Yake kudutsa mzakazi. Tangoganizani, Iye anakhoza kokha kumupeza munthu mmodzi wolungama mu nthawi ya Nowa. Mu nthawi ya Mose, Iye anangopeza munthu mmodzi wolungama.

194 Tayang'anani pa Samsoni. Mwaona, Mulungu akhoza kungogwiritsa ntchito chimene inu mwachipereka kwa Iye. Samsoni anali munthu wamkulu wamphamvu, iye anali ndi mphamvu zambiri. Samsoni anapereka mphamvu zake kwa Mulungu, koma iye sanapereke mtima wake. Iye anapereka mtima wake kwa Delila. Mukuona? Umo ndi momwe zikukhalira ndi anthu lero. Oh, m'bale, iwo amafikira ndi kulipira ngongole, ndi zinthu monga choncho, ndi kumanga chipembedzo chachikulu, ndi zina zotero monga choncho, koma, pamene zifika popereka mtima wawo, iwo samachita zimenezo. Uko nkulondola. Ndi zaubwino wanji . . .

195 Petro anali ndi lupanga. Iye anasolola lupanga limenelo,

anali woti adule makutu a wansembe wamkulu, ndi zinthu monga choncho, iye anachita zimenezo. Koma pamene zinafika pa kulimbika kwenikweni kwa Chikhristu, iye analibe izo. Iye anabwerera mmbuyo ndipo anamukana Iye. Nkulondola uko? Iye anakwanitsa kudula khutu la wansembe wamkuluyo ndi lupanga lake, ndithudi, iye ankadziwa momwe angaligwirire ilo. Koma pamene zinafika pofinya ndi nthawi yoti ayime pa Mawu a Mulungu, iye analibe kulimbamtima, ndipo mpaka anakana kuti ankamudziwa Yesu.

196 Ndi pamene izo ziri lero. Ife tiri ndi kulimbika komanga manyumba ndi kuyika mamillioni a madola mwa iwo. Ife tiri nako kulimbika koyika ma limba a paipi ndi mipando yofewa, ndi chirichonse, ndi kupita kumeneko ndi kumakatembenuka kuchokera ku malo ndi kupita kwina, ndi kuwapanga a Methodisti kukhala Abaptisti, ndi zina zotero, mmbuyo ndi mtsogolo monga choncho. Koma pamene zifika pa kulimbika kwa Chikhristu, kuti tivomereze Mawu, Uthenga wa Mulungu, ndi kuyima pamenepo pa Iwo, timakhala apang'ono. Ndiye miyala yanuyo ili ndi phindu lanji popanda mmisiri wamiyala kachiwiri? Si kulondola uko?

197 Mulungu akufuna khalidwe, osati umembala. Khalidwe! Elieza, pamene iye anapita kukatenga Mkwatibwi wa—wa—wa Isaki, iye anakhetsera thukuta mpaka iye anapeza khalidwe. Kumbukirani, Abrahamu anamuyika iye pamalo oyankhira monganso Mulungu watiyikira ife pamalo oyankhira, ndiko kulondola, ife atumiki. "Kasakeni Mkwatibwi Wanga!" Mulungu adalitse mtima wanu. Ine sindikufunafuna mamembala, ine ndikufunafuna angwiro mu mtima, mwaona, winawake amene ati adzakhulupirire Mawu.

198 Elieza anayang'ana, ndipo iye anaganiza, "Oh, ine sindingakhoze kuchita izi mwa ine ndekha. Pali udindo wochuluka kwambiri. Ine ndikuzindikira udindo womupeza Isaki . . . " Chimene, chiri choimira cha Mpingo, inu mukudziwa, Khristu; Rebekah, choimira cha Mkwatibwi. Ndipo Elieza anagwada pa mawondo ake ndipo anati, "Mulungu, Inu—Inu mukungoyenera kuti mundithandize ine." Ndipo pamene iye analozera kwa Mulungu, Mulungu anamuthandiza iye. Iye anapeza khalidwe.

199 Bwererani ku Mawu, m'bale. Bwererani kwa Mulungu. Musati mupereke chidwi chirichonse ku mpingo uwu umene inu mulimo. Inu mukhoza kukhala mmenemo ngati inu mukufuna kutero, ngati iwo angakuloleni inu. Koma, chinthu choti muchite poyambirira, ndicho, kubwera kwa Mulungu. Ndiko kulondola. Uwu ndi uvangeri wa m'nthawi-yotsiriza. Inde, bwana. Khalidwe!

200 Ndipo pamene iye anadzapeza kuti, ndiyeno pamene Elieza anadzapeza khalidwe limene linali mwa mkazi, Rebekah,

mkwatibwi wokongola wa Isaki, iye anamuuza iye za Isaki. Ndipo iye sanafunse kanthu kamodzi. Iye anakhulupirira mawu a wamthengayo, ndipo anakonzekera kuti azipita. Ndipo iwo anapita, anakawafunsa abambowo, iye anati, "Ingomufunsani iye, mtsikanayo ndi wa usinkhu. Mufunseni iye, mulole chigamulo chake chikhale momwemo."

201 Iye anati, "Ine ndipita." Kwa chiyani? Mwamuna yemwe iye anali asanamuwonepo, sankadziwa kanthu za iye. Komabe iye anali wokonzeka, chifukwa iye anali wokonzedweratu ndi wodzozedweratu kwa icho. Kulondola ndendende.

202 Kodi inu munazindikira mkaziyo akutsuka mapazi a Yesu? Iye sanapemphe konse mdalitso. Iye anangoyang'ana pamenepo. Ndipo apo, wachinyengo uyo akuyesetsa kumuseleula Iye, kunyozetsa khalidwe Lake. Ndicho chimene iwo nthawizonse ankayesetsa kuchita, kumupangitsa Iye kuwoneka wamng'ono. Anthu ena, inu mukudziwa, iwo ankamutsatira Iye basi kuti achite zimenezo. Iwo amatha kunena kuti, "Tsopano, yang'anani apa. Mbuye wabwino, ife tikudziwa kuti Inu ndinu munthu wamkulu wa Mulungu, Inu simuwopa kalikonse. Kodi ife tizipereka msonkho kwa Kaisara?" Mukuona? Zinthu zonsezo! Kuti, kungoyesetsa kuti apeze chinachake choti chidetse Dzina Lake, kuliyipitsa ilo. Ndipo Mfarisi uyu anamuitanira Iye kumeneko kuti akadye chakudya chamadzulo, chipembedzo chimenecho podziwa kuti iwo akanamuyitanira Iye kumeneko, iwo anali ndi chitsulo pa moto penapake. Monga wotchova njuga anganene, "Atabisa chinthu mmanja mwake." Iwo anali ndi chinachake chofanana.

203 Pamene inu mumuwona aliyense wonga ameneyo, yemwe amakudani inu, chifukwa chomusankha Khristu, ndiyeno nkumakubweretsani inu mkati, izo ndi mwinamwake kuti apeze ndalama zambiri pa inu, kapena kuchita chinachake, kapena kukugwiritsani inu ntchito mwanjira inayake. Mukuona? Palibepo ayi. . . Iwo sangakhulupirire Uthengawo. Iwo ali nanu inu kumeneko kwa cholinga chinachakenso. Inu mukuganiza kuti Khristu yemweyo samazindikira chinthu chomwecho lero? Ndithudi, Iye amatero.

204 Koma iwo anamubweretsa Iye mmenemo, ndipo iwo anati, "Tsopano ife titsimikizira zimenezo." Ndipo anamutengera Iye kumbuyo uko ndipo anamulola Iye kuti alowemo akununkha, sanamutsuke konse mapazi Ake, sanamulandire konse Iye. Atakhala pamenepo, mmene iwo ankayenda mmikanjo imeneyo, inu mukudziwa, kumabwera mmenemo kumene akavalo ndi zinthu zinkadutsa panjirapo mmasiku amenewo, tinjira tating'ono takale ito. Iwo onse ankayenda njira yomweyo. Mkanjo wawukulu umenewo ukutenga kununkha kumeneko, ndipo izo zinali pa Iye, ndipo iwo unkanunkha chifukwa cha fumbi ndi zinthu za pa msewu. Ndi kununkha kwakale, monga mu khola ndi zinthu. Ndipo izo zinali pa Iye, akupita

ku nyumba ya alendo ndi makapeti aakulu ofewa awo ali pansi, chirichonse. Iwo ankakhala ndi mtundu wina wa mafuta, iwo—iwo ankatsuka nkhope zawo ndi kutsuka mapazi awo, ndi kuwapatsa iwo masilipasi akuchipinda, monga, ndi kusamala masandasi awo. Kenako ankabwera umo atatha kuvala zonse ndi kukonzekeretsedwa, ndi kukonza tsitsi lake, ndipo ankabwera mkatimo. Ndiye iwe umakumana ndi alendo ako, ndipo kenako—ndipo kenako iwe—ndipo kenako iwe—iwe umawapatsa iwo moni ndi kuwakumbatira iwo. Iwo amakumbatirana wina ndi mzake pakhosi, ndi kupsyopsyonana wina ndi mzake pakhosi. Mukuona? Monga inu munamuwonera Joseph ndi ine kanthawi kapitako tikuyika mikono yathu mozungulira wina ndi mzake, tikusisitana wina ndi mzake. Ndipo iwo ankapsyopsyonana wina ndi mzake pa khosi. Koma Mfarisi ameneyo, atatha kumuyitanira Iye mmenemo, ndipo apo Iye anali atakhala kumbuyo uko, iwo sanamutsuke konse mapazi Ake, iwo sanachite kanthu kwa Iye, anamusiya Iye kuti akhale pamenepo kuti angomuseleula Iye.

205 Koma hule lina laling'ono losawuka lonyozeka, ali ndi ma tambala pang'ono omwe iye anakawapeza kunja uko mu njira yake yoyipa yokhalira moyo, iye anamuwona Iye atakhala pamenepo. Ndipo misonzi yaikulu inayenderera pansi mmasaya ake. Iye anapita kumusi uko ndipo anakatenga bokosi la mafuta onunkhira, ndi ndalama zonse zomwe iye anali nazo. Iye anazembera mwanjira ina ndipo anafika kumbuyo kumeneko, ndipo iye anagwera pansi pa mapazi Ake, ndipo iye anayamba kulira, tsitsi lake linagwera pansi. Ndipo—ndipo iye ankakhoza kulira ndi kumatenga lake. . . Iwo analibe chopukutira kuti apukute mapazi Ake, ndipo iye anali atatenga tsitsi ili ndi kumapukuta mapazi Ake. Ndi madzi okongola bwanji kwa mapazi Ake, misonzi ya wochimwa wolapa! Ndipo ngati Iye akanangosuntha phazi Lake, iye akanalumphira mmwamba. Iye sanali kupempha kanthu, iye anangowona kuti izo zinkasowekera kuti zichitidwe.

206 Kodi ife sitingachite zimenezo lero? Mai, ife sitikupempha kalikonse. Izo zikusowekera kuti zichitidwe, Uthenga ukusowekera kuti uzilalikidwa. Kaya ife tipeza khobidi, kapena chirichonse, sizimapanga kusiyana kulikonse. Ine sindinayambe ndatengapo chopereka mmoyo mwanga. Ichi ndicho chosowekeracho. Ichi ndicho cholingacho. Kudzipatula, ndipo mipingo imadana nawe, ndi china chirichonse, ndi kukuchotsapo iwe, ndi abwenzi ochepa okha omwe iwe umatengana nawo limodzi. Koma iwo ndi Uthenga. Iwo ukuyenera kupita, mosalabadira. Ine sindinayambe ndadziyikapo ndekha konse pa wailesi ndi maprogramu aakulu a pa televizioni pamene ine ndikanayenera kuti ndiziwapempha anthu ndalama. Ine sindingachite zimenezo. Ine ndikufuna kuti ndikhale m'bale wanu. Ine ndikufuna kuti ndizipita kumene

Mulungu. . . Ngati alipo anthu faivi kuno, ndipita kumeneko. Ndipita cha kuno, ngati alipo millioni, Mulungu andipangira ine njira yoti ndipiteko. Ndizo zonse. Kumangozikhala moyo izo mwa chikhulupiriro. Ndi momwe ife tonse tiyenera kumachitira. Ndipo, zikomo Mulungu, ambiri a iwo akuchita zimenezo, inu mukuona, mwanjira yomweyo. Izo nzoona, iwo akuchita zimenezo.

207 Tayang'anani pa mkazi wamng'ono uyu. Yesu sanasunthe phazi. Tayang'anani pa Mfarisi wachikulire uyu ataima pamenepo, anati, akuyesetsa kuti amuseleule Iye tsopano, anati, "Tsopano, ngati Iye akanakhala mneneri, Iye akanadziwa mtundu wa mkazi yemwe anali kutsuka mapazi Ake. Mukuona? Iye akanadziwa mtundu wa mkazi yemwe anali momuzungulira Iye. Mwaona, ndi Uyo pamenepo, izo zikusonyeza gulu lomwe Iye amachita nalo." Ndine wokondwa kwambiri ndi zimenezo. Eya. Iye ankadziwa. "Tayang'anani pamenepo mtundu wa gulu la anthu lomwe liri ndi Iye. Ndife olemekezeka. Ndife mamembala a mpingo. Ndipo, taonani, wochimwa wakaleyo pamenepo ali ndi Iye, mkazi uja, ife tikudziwa yemwe iye ali, iye amayenda mu msewu. Iye ali. . . " Inu mukudziwa zomwe ine ndikuzikamba. "Chotero apo, iye anali mkazi wa mtundu umenewo. Taonani, taonani, ndiwo mtundu wa anthu umene umamuzungulira Iye." Ndine wokondwa kwambiri. Ndine wokondwa kwambiri.

208 Ndicho chimene ine ndinali, inu mukudziwa. Ine ndinali munthu wa mtundu woterowo, osakhala wabwino, wochimwa. Ndipo mmodzi aliyense wa inu ali chomwecho, amene sanabwere kwa Iye. Iwe sumabwera kuti udzangokhala membala wa tchalitchi, iwe umabwera chifukwa pali chinachake choti chichitidwe. Yesu akusowa kuti azitumikiridwa, winawake akuyenera kuti akhale ali pamenepo. Tiyeni tichite zimenezo. Iye sanafunse konse, "Ambuye, kodi Inu mungandidalitse ine, kodi Inu muchita *ichi*?" Ayi, iye anangotsuka mapazi Ake ndipo anawapukuta iwo ndi tsitsi la mmutu mwake. Inu mukudziwa, ena a alongo athu akanayenera kuyima ndi mutu wawo kuti apeze tsitsi lokwanira kuti apukute mapazi Ake.

209 Ndipo apo panali tsitsi lake lokongola lopilingizikana litagwera pansi, ndipo iye anapukuta mapazi Ake. Ndi "*kupsyopsyona*" iye anali kupsyopsyona "*kupsyopsyona*" mapazi Ake mosalekeza monga choncho. Yesu anangokhala ndi kumamuyang'ana iye. Iye sanasunthe inchi. Patapita kanthawi, pamene iye anatsiriza, Iye anatembenuka.

210 Apo panali Simoni wachikulire atayima pamenepo ali ndi gulu lonse la azitumiki, anati, "Mukuona! Ha! Ha! Ndi Ameneyotu. Mwaona, ndi zimenezotu, izo zikusonyeza chimene Iye ali. Iye si mneneri. Tayang'anani pa Iye!"

211 Iye anatembenuka ndipo anati, "Simoni!" Oh, ine

ndikuganiza kuti iye anali atafiira pa nkhope. Iye anati, "Ine ndiri ndi chinachake choti ndinene kwa iwe. Iwe unandiitana Ine kuno. Mukuona? Pamene ine ndinalowa pakhomo, iwe sunatsuke konse mapazi Anga, iwe sunandipsyopsyone Ine ndi kundilandira, iwe sunadzoze mutu Wanga. Iwe unangoyima pamenepo, ndi kumayesetsa kuti uzindisereula Ine. Mukuona? Iwe unandibweretsa Ine kuno kwa cholinga chimenecho. Ndipo mkazi uyu, chibwerereni ine, chibwerereni ine, iye mosalekeza wakhala akutsuka mapazi Anga ndi misonzi yake, ndi kuwapukuta iwo ndi tsitsi la mmutu mwake. Ndipo iye mowirikiza, osati kupsyopsyona pa khosi Langa, koma wakhala akupsyopsyona phazi Langa."

"Iwe sunayembekezere kanthu, sichoncho iwe, mlongo?"

"Ayi."

212 "Koma ine ndikunena kwa iwe kuti machimo ako, amene ali ambiri, onse akhululukidwa." Uh-Huh. Eya. Mukuona? Njira yonse mpaka mmusi iye analibe kalikonse nkomwe, koma basi mantha kuti iye sanali kuchita chinthu choyenera, mwinamwake, koma izo zinkasowekera kuti zichitidwe, koma mphotho yake inabwera pa mapeto.

213 Inu mukhoza kumandimva ine ndikulalikira Uthenga uwu. Inu mukhoza kumauwona Mzimu Woyera ukuzindikira ndi kuchita zinthu zazikulu, ndi kumachita zozizwitsa. Inu mukhoza kumapemphera, ndipo izo osakwaniritsidwa konse. Pitirizani, mphotho yanu idzabwera pamapeto. Kodi zimenezo sizingakhale zabwino pamenepo pomwe? Eya. Mwaona, muchitireni Yesu utumiki. Umenewo ndi Uthenga wa m'nthawi-yotsiriza. Iye anali ndi Mkwatibwi. Mulungu akufuna khalidwe. Ndiyeno Elieza atatha kupeza khalidwelo, ndiye chinthu chotsatira chinali kumukonzekeretsa iye kuti azipita. Ndicho chimodzimodzinso pano, m'bale, chimodzimodzi tsopano. Uthenga wa m'nthawi yotsiriza suli kunja uko mu Babeloni.

214 Apo ndi pamene ine ndinanena kwa iwe, Joseph, pamene m'bale wanga wamng'ono wachi Swede uyu anayima kunja uko ndipo anaika mutu wake pa phewa langa tsiku lina ndipo analira ngati mwana wamng'ono. Iye anati, "M'bale Branham, Mulungu ananditumiza ine kuno, Chicago, anati ndimafuna ndidzawone Chicago akugwedezeka limodzi la masiku amenewa." Ndipo iye anati, "Tsopano iwo akundithamangitsa ine. Iwo akuwutenga mpingo wanga kuwulanda pansi pa ine, mpingo waukulu, wabwino kwambiri mu Chicago." Anati, "Iwo akuwutenga mpingo wanga, ndipo apa iwo andithamangitsira ine kunja. Iwo andichotsa ine. Ine sindikudziwa choti ndichite."

215 Ine ndinati, "Joseph, Mulungu samanama." Ine ndinati, "Iwe wamuwona Chicago akugwedezeka. Izo zinayambira ku Mzinda wa New York pamene ine ndinakuwona iwe kumeneko, chifukwa iwo sankagwirizana nawe iwe, ine sindikanapitako nkomwe."

Ndipo sanamudziwe iye nkomwe, koma chinachake chokhudza iye chimene chinandikokera ine kwa iye. Ine sindikunena izi chifukwa msonkhano wake wa umishonare uli usikuuno. Koma, izo zinali kulondola, ine ndinakokedwera kwa Joseph. Ine ndinakana kupita ku Chicago, chifukwa iwo sankamulola iye kuti abwere, sankamulola iye kuti abwere mu mgwirizano. Ine ndinati, "Ndiye ine sindipitako nanenso."

Anati, "Iwe sukumudziwa iye."

216 Ine ndinati, "Ine ndikudziwa kuti sindikumudziwa iye, koma Mulungu akumudziwa iye. Iye ndi wantchito wa Mulungu. Ndipo, kwa ine, iye ndi wabwino bwino."

Ndipo kotero Joseph anati, "Ine ndikanakonda ndikanamuwona Chicago akugwedezeka."

217 Oh, mai! Sakuzindikira kuti akugwedezeka koma sizikutanthauza utuchi wa akasinja uja kunja uko. Izo sizikutanthauza zinyalala izo zimene zidzawonongedwe kunja uko. Mpingo ukugwedezeka. Mukuona? Analipo handiredi ndi twente okha kuchokera ku mamillioni, mu chipinda chapamwamba, pamene kugwedezako kunabwera. Uko nkulondola. Ndithudi. Ndi kugwedezeka, ndi anthuwo. A . . .

218 Taonani, pamene iwo ankakhala ndi chitsitsimutso chachikulu chija, Apollo uyu, mlaliki wa Chibaptisti yemwe anali asanalandire Mzimu Woyera apabe, anali asanabatizidwepo mu Dzina la Yesu Khristu. Paulo akudutsa mmagombe akumtunda aku Efeso, iye anawupeza mpingo wamphamvu uwu umene Baibulo limawukamba, ndipo iye anapita kumeneko ndipo anakawauza iwo njira ya Ambuye. Ndipo iwo anati. . . Iye anati, "Kodi inu munalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni chanu?" Ndipo iwo anali akufuula ndi kumakhala ndi nthawi yopambana. Anati, "Kodi inu munalandira Mzimu Woyera?"

Anati, "Ife sitikudziwa ngati ulipo uliwonse."

Anati, "Ndiye inu munabatizidwa motani?"

Iwo anati, "Ife tinabatizidwa pansi pa Yohane."

219 Iye anati, "Izo sizikugwiranso ntchito pano. Mukuyenera kuti mubatizidwenso." Ndipo iye anawabatizanso iwo, mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo anayika manja ake pa iwo, ndipo Mzimu Woyera unadza pa iwo. Iwo anayankhula mmalirime ndipo analosera. Ndipo uko kunali pafupifupi eyiti kapena teni a iwo. Uko nkulondola.

220 Kugwedeza! Mwaona, Mulungu samagwedeza zimenezo, gehena idzagwedeza zimenezo pamene iyo idzalandire izo. Koma Mulungu amawugwedeza Mpingo Wake.

221 Mngelo mmodzi anabwera kwa Abrahamu ndi gulu lake pamwamba pa phiri, ndipo anadzachita chozizwitsa, pozindikira malingaliro amene anali mu mtima mwake.

Nkulondola uko? Ndipo Sarah ali mkatimo. Kumene, angelo omwe anapita ku Sodomu anali nawo masauzande kumusi uko. Mwaona, kugwedezako kumabwera mu gulu laling'ono. Iwe waziwonapo izo, Joseph. Iwe wamuwona Chicago akulandira kuyitana kwake kotsiriza. Uko nkulondola. Ndipo Mulungu anakulemekeza iwe, anachita ndendende basi zimene Iye ananena. Kumukonzekeretsa Mkwatibwi, ndicho chimene icho chiri.

222 Tsopano ife tikuti titsirizire pomwe pano, ponena izi. Uthenga wa m'nthawi-yotsiriza uli woti umukonzekeretse Mkwatibwi ndi kukonzekera Mkwatulo. Kodi izo zingachite chiyani? Malingana ndi Malaki 4, akuwabwezeretsa iwo kubwerera ku Chikhulupiriro chimene chinaperekedwa kamodzi kwa oyera mtima. Kuwabwezeretsa iwo ku Chikhulupiriro cha makolo, gawo la chipentekoste, mu nthawi ya kubwezeretsa. "Ine ndidzabwezeretsa, atero Ambuye." Ndicho chochitika chenicheni, uvangeri wa m'nthawi-yotsiriza.

223 Tsopano ine ndikungofuna kunena mawu angapo awa ndisanatseke. Ine ndinalambalala Malemba ena onse awa, ndipo mwinamwake nthawiyina ndikhoza kudzafika kwa iwo. Koma ine ndikufuna kunena ichi. Ife tikukhulupirira kuti ife tiri pa nthawi yotsiriza. Ife timakhulupirira zimenezo. Ndipo ngakhale izo zikuwoneka ngati pa nthawi yotsiriza, pa nthawi ino, kuti Uthenga ndi Wamthenga ziwiri zonse zatsala pang'ono kusweka. Zikuwoneka ngati Satana wayesetsa mwa kuthekera kwake kuti atiwononge ife. M'bale Neville, ngozi yake; M'bale Crase pamenepo; ndi mfuti ikuwombera izo. Mwaona, izo zikuwoneka ngati, ndipo pakali pano pamene mpingo uliwonse kudutsa uko wandikana ine. Ndipo, mwaona, mwaona, zikuwoneka ngati ziri—ziri pafupi kusweka. Zikuwoneka ngati ife tagonjetsedwa. Inu musadandaule. Inu mukudziwa, kawirikawiri imakhala nthawi imeneyo imene Mulungu amabwera powonekera, za chinachake chimene Iye wakhala akupenyerera kwa nthawi yaitali. Inu muzikumbukira.

224 Kumbukirani nthawi ina kunali ana ena uko mu ng'anjo ya moto, iwo anali akugwiritsitsa moona ku Mawu amenewo. Chirichonse chinalakwika. Iwo anawaponyera iwo mu ndende. Iwo anawasunga iwo usiku wonse, iwo anali woti awawotche iwo mmawa wotsatira. Ndipo zinkawoneka ngati mapeto anali pafupi, iwo anali akuyenda mpaka ku ng'anjo komwe. Koma Iye anadzabwera akutsikira pansi kuti adzasinthe, chochitikacho chonse chinasinthidwa mu kamphindi chabe.

225 Izo nthawizonse zimachitika mu nyengo zofooketsetsa zimenezo, pamene izo zikuwoneka ngati Uthenga woona uli pafupi kugonjetsedwa, ndi pamene Mulungu amadzabwerapo. Iye—Iye amawulola Uthenga ndi mtumikiyo kuti afike kumapeto a msewu, mwaona, kenako Iye amadzabwera umo ndipo Iye amakwera mafunde aakuluwo. Zoona zimenezo.

226 Kumbukirani, anali Yesu, pamene adani Ake ankaganiza kuti iwo anali atamugonjetsa Iye, wosakhulupirira anati, "Ife tamufikitsa Iye pa mtanda." Asaduki ndi Afarisi amene ankamuda Iye ndi kumupachika Iye ku mtanda, iwo ankaganiza, "Ife tamupeza Iye tsopano." Huh-uh. Inali pafupifupi nthawi imeneyo pamene Mulungu anabwera powonekera, anamuwukitsa Iye mmawa wa Isitara, ndipo anaswa maufumu a Satana, anamuvula gehena, anatenga makiyi a imfa ndi hade, ndipo anawuka limodzi nawo. Zedi, izo zinali basi pa nthawi yofooka imeneyo. Uthenga Wake, Iye anali atalalikira Mawu, Iye anali ataima pafupi, ndi chirichonse, ndiye inali mphindi yofooka kwenikweni iyo pamene chigonjetso chinadzabwera. Pamene Iye anachita zonse zomwe Iye akanakhoza kuzichita, kenako Mulungu anadzabwerapo. Iye anasintha chochitikacho.

227 Anali Yakobo akumuthawa Esau, kuzembera *apa* ndi *apo* (uko . . . ? . . . , ndi osiyanasiyana awo) poyesetsa kuti abisale kwa Esau. Kenako mtima wake unayamba kulakalaka kupita kwawo. Ndipo ali pa ulendo wake wopita kwawo, iye anatumiza amithenga, iye anatumiza zopereka ndi china chirichonse, kuyesetsa kuti amusangalatse Esau. Koma panali pamene Yakobo anafika kumapeto kwa iyemwini, ndi pamene Yakobo sankadziwa njira yoti atembenukire. Iye anawolotsa mkazi wake ndi ana pa—madzi, ndipo iye anawoloka kubwereranso—mtsinjewo. Panali pamene Yakobo analimbana usiku wonse, mpaka mphamvu zake zinali zitatha, ndipo iye anali atalumala ndipo iye anali wofooka, ndipo thupi lake linasweka. Inali nthawi imeneyo pamene Mulungu anadzabwera powonekera. Mmawa wotsatira, ife tikumupeza iye ali chiyani? Kalonga wopanda mantha, pambuyo pa kufooka kwake. Izo zinkawoneka ngati iye anagonjetsedwa. Koma ife tikumupeza iye ali kalonga wopanda mantha. Uthenga unali ukupitirira, ndipo mtumikiyo anali nawo iwo. Ndiko kulondola ndendende. Iye anali kalonga wopanda mantha tsiku lotsatira.

228 Esau, ngakhale, pamene iye ankamusowa iye moyipitsitsa, Esau, pamene iye anakomana naye iye. Ndipo kumbukirani, nthawi yomweyo Mulungu ankagwira ntchito pa mtima wa m'bale wake, nayenso. Uko nkulondola. Ndipo Esau anabwera kwa iye, anati, "Ine ndiri nawo ankhondo kuno." Anati, "Ah, ndiwe wofooka, Yakobo. Thupi lako likusautsika. Iwe wasweka." Anati, "Ine—ine—ine . . . Ine nditumiza asilikari kumeneko kuti adzakuteteze iwe," nthawi yomweyo imene iye ankawasowa iwo.

229 Koma iye anali atapeza chinachake. Anati, "Ine ndipita ndekha." Ameni. Ndi pamene iye anachira ku kufooka kumeneko, iye anali atachira ku mantha amenewo.

230 Pamene Yesu anachira ku mantha a imfa, Iye anali wamphamvu kwambiri, Iye ankakhoza kudutsa pa khoma popanda ngakhale kusuntha matope a mwalawo. Iye ankakhoza kudya nsomba ndi mkate. Ameni. Oh, inde. Inali nthawi

imeneyo, kufookako kutabwera, kuti anadzipeza yekha ali wamphamvu. Izo zinali pambuyo pa kufookako kutabwera.

231 Ndipo zikuwoneka ngati ndi zofooka kwambiri tsopano kwa zonse Uthenga ndi wamthenga. Koma inu musadandaule! Kwinakwake, ine sindikudziwa motani, koma ine ndikumudalira Iye. Iye adzabwera powonekera tsiku lina. Inu musadandaule. Tiyeni tipite limodzi. Tiyeni tiweramitse—tiyeni tiweramitse mitu yathu limodzi. Uvangeri wa m'nthawi yakumadzulo.

232 O Mulungu, Kuwala kwakukulu kwakumadzulo kwakhala kukuwala tsopano kwa nthawi yaitali. Ife takuonani Inu mukuyenda kudutsa mmipita iyi kuno, mukuwabweretsa iwo amene anangokhala mithunzi chabe ya amuna ndi akazi, atadyedwa ndi khansa, akhungu, odwala ndi osautsika, madokotala ochokera ngakhale ochokera kwa a Mayo ndi kulikonse atawalephera iwo. Tsopano iwo akhala pano mmawa uno, ndipo ambiri a iwo athanzi ndi amphamvu. Osati kuno kokha, koma kuzungulira dziko. Akazi alandira ana awo atawukanso ku moyo, atafa kale kwa maora. Ana ataphedwa pa msewu, ndi magalimoto, atalengezedwa kuti "afa" ndipo atagonekedwa pansi, opanda fupa labwino mwa iwo; ndipo mu nthawi ya miniti nkukhala akuyenda mu msewu, akutamanda Mulungu. Inde, Ambuye, Ndinu Mulungu. Nthawi ya kumadzulo ili pano. Mbewu za uvangeri zakumadzulo zafesedwa, Atate, ndipo tsopano zikuwoneka ngati zikukhala ngati ikubwera nthawi yolumalitsa. Ambiri a awa . . .

233 Pamene Inu munadza koyamba powonekera kumbuyo uko mu nyengo Yanu, onse a iwo, "Mneneri wamng'ono uja wa ku Galileya!" Oh, iwo onse anasonkhana mokuzungulirani Inu. Koma pamene Inu muyamba kuwakantha iwo ndi kuwauza iwo za tizikhulupiriro tawo ndi—ndi zinthu, ndiye iwo anachoka kwa Inu. Inu munkayenera kuyima nokha. Ndipo potsiriza iwo anakutengerani Inu ku Kalvare. Izo zinkawoneka ngati iwo anali atapambana, zinkawoneka ngati awo—gulu lawo lalikulu laluntha linali litagonjetsa cholinga cha Mulungu. Koma, oh, ayi! Mmawa wa Isitara dziko lapansi linali ndi manjenje, manda anatseguka ndipo Mwana wa Mulungu anawuka. Iye anali ndi makiyi a imfa ndi hade. Iye anali ndi ubatizo wa Mzimu Woyera mkati mwa maufulu Ake kuti awupereke pamenepo. Iye anawuwuza Mpingo Wake, "Pitani uko ku Yerusalemu ndipo mukayembekezere, ndipo Ine ndidzatumiza Iwo pa inu, ndipo kenako inu mudzandichitira umboni Ine kufikira Ine ndidzabwererenso kachiwiri."

234 Ndiyeno Inu munayima ndi kuwauza iwo momwe nthawi ikanadzakhalira, ndipo pano ife tiri mu nthawi yotsiriza. Ambuye, bwerani mkati kachiwiri, kodi Inu simutero, Atate? Ife tikutopa, otopa. Munthu watikana ife kuchokera konsekonse, zipembedzo zonse zakana. Ku California uko, oyera ofunika

awo atayima kunja uko akulira, mipingo forte, ndipo mtsogoleri mmodzi uyo anaimirira ndipo anati, "Chabwino, ngati iye amabatiza, pogwiritsa ntchito Dzina la Ambuye Yesu, ife sitikumufuna iye." Ndipo anawubweza Uthenga kuchoka kwa anthu osauka anjala amenewo.

235 Ndipo, Atate, ine ndinati, "Bwerani mudzakomane nane ndi Lemba," ndipo iye sanachite izo. Chifukwa chiyani? Iye akudziwa bwinoko. Atate, nchifukwa—nchifukwa chiyani achikunja anakwiya ndipo anthu nkumaganiza kuti nzopanda pake? Moonadi potambasulira dzanja la Mwana Wanu Woyera Yesu, kuchiza odwala, ndi kuwonetsera zizindikiro ndi zodabwitsa za kumapeto. Izo zabwerezedwanso, Ambuye. Ine ndikuwapempherera iwo. Mulungu, musalole kuti iwo atayidwe kutali. Adakalimo anthu ambiri a iwo abwino mmenemo panobe. Perekani, Ambuye, kuti iwo awone ndi kutulukamo.

236 Ndipo osonkhana athu aang'ono mmawa uno, Atate, ife sitikuidziwa mitima ya anthuwa. Inu mukuidziwa. Gulu laling'ono ili kuno. Ine ndikupita uko komwe, mulimonse. Ndipo tsopano ife tisanachoke mu tchalitchi, Ambuye, gulu laling'ono ili limene likuyenda kuno, iwo ndi amwendamnjira. Iwo samadzinenera kuti ndi a mdziko lino, Ambuye. Iwo ndi alendo. Iwo abadwa mwatsopano, iwo ndi zolengedwa zatsopano. Iwo abwera kuchokera ku zinthu za mdziko, kuti adzamutumikire Mulungu, podziwa kuti, "Sitisirira chuma chachabe cha dziko lino chimene chimawola mofulumira. Ife tiri ndi ziyembekezo zathu zitamangidwa pa zinthu Zamuyaya, izo sizidzatha konse."

237 Atate Akumwamba, ngati pangakhale mwa mwayi mmodzi kapena kupitirira pakati pathu mmawa uno amene sanayambe akhalapo ndi kumverera konga kuti iwo ayenera kupanga kutembenuka kumeneko, ine ndikupemphera kuti Inu muyankhule kwa mitima yawo pa nthawi ino. Ndipo mulole kuti iwo mokoma ndi modzichepetsa, mmitima mwawo, angopereka zonse kwa Inu, ndi kuti, "Ambuye Yesu, mundichitire ine chifundo, wochimwa. Ine sindikufuna kuti ndife mu chikhalidwe chimene ine ndirimo tsopano. Ndipo posadziwa kuti ndikhala ndi moyo ngakhale kudutsa mu tsikuli, ndiye sikuli kupusa kutaya nthawi yanga pazinthu za mdziko!" Ndipo chirichonse kuno chidzawonongeka, ndipo anthu adzawonongedwa limodzi ndi dziko. Koma Mulungu, Atate Wamuyaya, sangakhoze kuwonongeka, ngakhalenso anthu Ake. Mulole iwo avomereze Izo tsopano, Atate athu Akumwamba.

238 Yeretsani mipango iyi ili apa kwa odwala ndi osautsika. Iwo anati iwo ankatenga kuchokera mu thupi la Paulo, mipango ndi zovala, mizimu yoipa inkachoka kwa iwo. Chiritsani odwala amene ali pakati pathu mmawa uno. Ine ndikupemphera kuti pasakhale munthu wofooka pakati pathu.

239 Mulole Mzimu Woyera waukulu uyende kudutsa mwa

omvetserawa tsopano, ndipo mulole kuti aliyense azindikire Kukhalapo Kwake. Ndipo monga ndinanenera poyamba, pamene namondwe akudza mu chirimwe chowuma, mphepo imakhala ili yowuma ndi yotentha, fumbi limakhala likuwuluka, koma, zonse mwakamodzi, ife tikhoza kumva bingu, ife tikhoza kuwona mtambo ukubwera. Ndipo ine ndinati chizindikiro chofiira chiri pansi, Iye akubwera. Ndipo ife tikumverera mphepo yozizira, kulandiridwa kwa Mzimu Woyera pamene Iwo ukuyenda kudutsa mmalo athu owuma. Tithandizeni ife lero. Mupulumutse otayika. Mutidzadzitse ndi Mzimu Woyera, Ambuye, mwamsanga, kuwalako kusanazime, pakuti chizindikirocho chiri kale pansi. Chombo chakale cha Zioni chiri mu zokonzera tsopano, ndipo sipatenga nthawi yaitali mpaka icho chikhala chikuitana. Ndipo, zonse mwadzidzidzi, iwo adzakhala akutululutsa nyuzipepala, "Chinachitika ndi chiyani? Mahandirede a anthu kudutsa mfukoli asowa."

240 O Mulungu, ndiye idzakhala nthawi itatha kwambiri kwa ena onse a iwo, mkwatulo udzakhala utabwera. Chiweruzo chidzakantha dziko lapansi, olungama adzakhala atapita. Ndiye iwo azidzapita ku manda, ndi kukati, "Chabwino, kodi sizinati . . . Kodi iwo anadzatsegula manda awa? Chabwino, kumachitika chiyani kuno?" Oh, iye amene ankadalira mwa Mulungu, yemwe anafa zaka zapitazo, adzakhala atapita kale. "Ndiye, oh, kudzakhala kulira ndi kubuula kotani pamene otayika adzauzidwe za tsoka lawo. Iwo adzalirira kwa mathanthwe ndi phiri," molingana ndi Malemba, "adzapemphera, koma mapemphero adzakhala atachedwa kwambiri." Mulole kuti izo zisadzakhale chomwecho ndi aliyense amene ali pano lero.

241 Ndipo ife tidakali ndi mitu yathu yoweramitsidwa, mitima yathu yoweramitsidwa, nayonso. Ndine munthu wosamvetseka kwambiri pankhani yoitanira anthu ku maguwa, ine ndimakhulupirira kuti si chiphunzitso chautumwi. Ine ndimakhulupirira kuti pomwepo pamene inu mwakhalapo mupange chigamulo chanu, kaya inu mukufuna kwenikweni kuti mukhale moyo kapena mufe. Ine ndikukhulupirira kuti ziri kwa inu. Ndipo ngati pali winawake pano yemwe sanaziwonepo izo kwenikweni mwanjira imeneyo, ndipo wazindikira ora limene ife tirimo, ndipo inu mukungofuna kuti ine ndikukumbukireni inu mu pemphero, kuti inu mukufuna kuti mukhale Mkhristu, ndipo inu mukufuna kuti mukhale monga Khristu mu moyo wanu ndi kukhala okonzekera kudza Kwake, kodi inu mungangokweza manja anu kuzungulira mchipinda chino. Ambuye akudalitseni inu, ndipo akudalitseni inu, ndipo akudalitseni inu, ndi inu, ndi inu. Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko kumbuyo, akudalitseni inu kumusi kuno. Ndizo zabwino. Mulungu akudalitseni inu, dona wamng'ono, pa mphambano pomwe pa moyo,

mlongo. Chimenecho ndi chigamulo chopambana. Inu mukhoza kukhala kuti munachitapo zochuluka kwambiri. . . Mulungu akudalitseni inu, adadi. Inde, inu mukhoza kukhala kuti mwagwira ntchito masiku ovuta ambiri mmoyo wanu, inunso, ndipo mwalera mwana wamng'ono. Amayi, inu mwakhala pafupi ndi iye. O Mulungu! Mwinamwake inu mwalera banja lanu ndi kuchita zinthu zazikulu zambiri, mumasisita masaya a mwana pamene anali kulira, munkasunthasuntha pogonapo ndi manja anu aang'ono, tsopano iwo ndi okalamba ndi ofooka. Zikhoza kukhala kuti munamusamalira mwanayo ndi kumuchitira zabwino zambiri, koma chinthu chopambana kwambiri chimene inu munayamba mwachitapo chinali pamene inu munakweza dzanja lanu pamenepo. Iye anakuwonani inu. Mundikhululukire ine, chonde.

242 Atate athu Akumwamba, Inu mwawona manjawo. Inu mukudziwa chimene chinali kumbuyo kwawo. Tsopano iwo ndi zikho za msonkhano uno. Iwo ndi zikho za Uthenga. Inu munati, "Onse amene Atate andipatsa Ine adzadza kwa Ine, ndipo palibe munthu angakhoze kubwera kupatula Atate Anga atamukoka iye poyamba." Ndipo Inu mwayankhula kwa anthu awa. Ndipo iwo anali atakhala pamenepo, ndipo molingana ndi sayansi iwo sakanakhoza. . . manja awo akuyenera kukhala pansi, chifukwa mphamvu yokokera pansi imawakokera iwo pansi. Koma iwo anaswa ndi kunyoza malamulo a sayansi. Iwo ali ndi Mzimu mwa iwo umene unakweza dzanjalo, umene uli wosiyana ndi sayansi, chifukwa Mzimu uli mmenemo ukhoza kuswa sayansi. Ndipo iwo anakweza dzanja lawo chifukwa panali Mzimu wa Mulungu powazungulira iwo, umene unati "Iwe uli. . . iwe ukusowa Khristu." Ndipo iwo anakweza mmwamba manja awo, "Mundikumbukire ine, O Ambuye."

243 Monga wakuba uja akufa pa mtanda, anati, "Mukandikumbukire ine pamene Inu mukubwera mu Ufumu Wanu."

244 Ndipo kodi Inu munanena chiyani kwa iye? "Lero iwe ukakhala ndi Ine mu Paradizo."

245 Ndipo ine ndikupemphera, Atate, kuti tsiku lomwe lino kuti Inu muwatengere mu Ufumu Wanu, kulowa mu chiyanjano Chanu kuno ku dziko lapansi, mmodzi aliyense wa okhulupirira awa, ndipo mukhale achifundo kwa iwo. Yesu, Inu munati, pamene Inu munali kuno ku dziko lapansi, mu Yohane Woyera 5:24, "Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene ananditumа Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya; ndipo sadzabwera ku chiweruzo, iwo sadzakhala kumeneko pamene chiweruzo chidzakhala chikukantha dziko lapansi, koma iwo adutsa kuchoka ku imfa kupita ku Moyo." Inu munalonjeza izo, Ambuye. Ine ndikuwatenga iwo. Ndipo tsopano kwa onse amene anakweza manja awo, ndipo ngakhale iwo amene mu mtima mwawo anakhulupirira kuti iwo amayenera kutero,

ndipo sanatero, ine ndikuwapereka iwo kwa Inu mmawa uno, Atate, monga zikho za chisomo cha Yesu Khristu ndi cha Mawu Ake omwe ife tawalalikira mmawa uno. Iwo ndi Anu. Asungeni iwo motetezeka, Ambuye, kufikira tsiku limenelo. Ndipo mulole kuti iwo akule ngati makanda. Mulole madziwa apa mu dziwe awapeze iwo, pamene iwo avomereza machimo awo, atafa, atayikidwa mwa Khristu, kuti awukenso kachiwiri ku moyo watsopano, kuti aziyenda mu dziko latsopano, kumayenda ndi oyanjana nawo atsopano, kumayenda mu gulu latsopano, kumayenda ndi angelo, kumayenda mu Kukhalapo kwa Chauzimu. Zinthu zimenezo zimene iwo sangathe kuziwona powazungulira iwo, koma iwo amazimverera ndi kudziwa kuti izo ziri pamenepo. Izo ndi zinthu zokhalitsa, Chauzimu ndi chokhalitsa. Ife tikuwapereka iwo kwa Inu Atate, mu Dzina la Yesu. Ameni.

246 Tsopano, ine ndikupepesa chifukwa chokusungani inu mopitirira nthawi pang'ono, ndipo ine ndikutsimikiza kuti inu. . . Inu mukumverera bwino? Tsopano, msonkhano, nthawizina ine ndimayenera kuti ndidule ndi kufinya. Tsopano kwa inu amene munakweza manja anu ndipo mukukhulupirira pa Ambuye Yesu, iwo akhala ndi utumiki wa ubatizo, ine ndikuganiza, madzulo ano. Kapena, inde, ine ndikuganiza kuti madziwe adzaza ngati inu mukufuna izo pakali pano, ndipo mikanjo ndi zina zotero zakonzeka. Ngati inu mukukhumba kuti mubatizidwe pakali pano, nthawi iliyonse, ife tiri pano kokha kuti tichite zimenezo. Ndipo tsopano titatha kudula ndi kucheka. . .

247 Ife—ife tikukuthokozani inu alendo mkati mwa zipata zathu, chifukwa chobwera kudzayanjana nafe mmawa uno pozungulira Mawu a Mulungu, ife tikuyamikira chifukwa cha kubwera kwanu. Ambuye akudalitseni inu. Ndife okondwa kwambiri chifukwa chakuti inu munali pano.

248 Ine ndikumuwona mzanga wa ine wakhala kumbuyo mchipinda muno, amene ine sindinamuwone kwa nthawi yaitali. Ine sindikudziwa nkomwe dzina la mnyamatayo. Iye ndi mzanga wabwino wa ine. Iye ndi msuweni wa mtsikana yemwe ine ndinkayenda naye, Marie Francisco. Ine sindingakhoze kuganizira kuti ndi ndani kapena lomwe dzina lake liri. Kodi mungakweze dzanja lanu? Ndife okondwa kukhala nanu inu mutakhala apo ndipo Mulungu akudalitseni inu. Mnyamata ameneyo wakhala ali Mkhristu kwa zaka zambiri. Ndipo ndine. . .

249 Mzanga kuno, Jim Poole, ndi angati anayamba andimvapo ine ndikumutchula Jim Poole, mzanga waunyamata, mwana wake wamwamuna ndi mkazake.

250 Ndi Donny, ine ndikulephera kuganizira za dzina lake lomaliza. Gard—Gard, Donny Gard ndi mkazi wake

wokondedwa wamng'ono apa. Iwo anali ali kunyumba dzulo kuti adzandichezere ine. Ndife wokondwa kwambiri kukhala nawo iwo mmawa uno.

251 Ndipo ine ndikukhulupirira kuti uyu ndi m'bale wachirendo wakhala pomwe apa pafupi ndi M'bale Way. Ndipo, oh, chotero, pomwe pano, mwinamwake ine ndikulakwitsa, ndipo nthawizina ine ndimaiwala nkhope. Ndipo ndine wokondwa kukhala nanu nonse muno mmawa uno.

252 Ndipo tsopano, ife tisanachoke, titatha kudula . . . Ndipo, inu mukudziwa, Baibulo linati Mawu a Mulungu . . . monga chigamulo chimenecho, kupanga mwala, koma iwe umayenera kukhala ndi wosema miyala kuti awudule iwo, kuti apange mawonekedwe ake. Mukuona? Ndipo Ahebri mutu wa 4 anati, "Mawu a Mulungu ndi akuthwa kwambiri ndi amphamvu kwambiri kuposa lupanga lakuthwa konsekonse." Iwo amadula, amachita mdulidwe, amadula zowonjezera. "Ngakhale ozindikira maganizo ndi zamkati mwa mtima," Mawu a Mulungu. Ndipo Iwo amadula.

253 Tsopano, basi kuti tipembedze, tiyeni tingoyimba nyimbo yanga yaying'ono yachikale imene ndimaikonda, imodzi mwa zomwe ndimazikonda, "Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye." Ndi angati akumukonda kwenikweni Iye? Ine sindikusamala kaya ndinu Mkhristu kapena ayi, inu munene "Ine ndimamukonda Iye chifukwa Iye anayamba kundikonda ine." Tiyeni tiyimbe iyo pamodzi tsopano, tonse pamodzi.

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

254 Kodi inu simukuzikonda zimenezo? Tiyeni tiyimbe iyo kenanso. Pamene inu mukutero, gwiranani chanza ndi winawake pozungulira inu. Musati mudzuke, mungoti, "Mulungu akudalitseni inu, m'bale," winawake pafupi nanu, chomwechonso inu, aliyense amverere kulandiridwa kwenikweni. Uko ndi kukulandirani kwathu kuno ku kachisi, kuchokera kwa ine, aliyense wa inu. Chabwino.

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye

Mulungu akudalitseni inu, m'bale.

Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

255 Tiyeni tiweramitse mitu yathu pamene ife tiziying'ung'udza iyo. Tsopano kwezani dzanja lanu kwa Iye, mophweka ndithu. Tsopano, kodi Iye si wodabwitsa? Inde.

256 [M'bale akuyankhula mmalirime. M'bale Branham akuimikira—Mkonzi]. Molemekeza kwenikweni basi mphindi chabe.

Yesu anati, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Iwo adzayankhula ndi malirime atsopano. Ngati iwo adzatenga njoka kapena kumwa chinthu chakupha, izo sizidzawapweteka iwo, pakuti ngozi kapena kuphulika sizidzawapweteka iwo. Iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira."

Inu mungodikira miniti, muwone ngati kutanthauzira kwina kukubwera kwa ichi. Ngati alendo ali mu zipata zathu, ife tikuyembekezera kuti tiwone chimene Ambuye ati anene kwa ife kudzera mu uthenga uwu.

[M'bale akutanthauzira—Mkonzi]. Kutanthauzira. Ameni. Uko ndi kutanthauzira kwa zomwe mwamuna uyu ananena. Kwa anthu pano amene mwina sangakhoze kudziwa chimene icho chiri, Iwo ndi Mzimu. Izo zimachitika kawirikawiri mu kachisiyu, kupereka uthenga kwa anthu.

Tiyeni tipemphere.

257 Atate Akumwamba, ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha ichi, posadziwa kuti winawake kwinakwake, kuti Inu munayankhula kwa mtima kwinakwake ndipo Iwo unayitaniranso kachiwiri, ngakhale mu uthenga wotsekera, Iwo unati, unawatcha iwo Anu "anawo," chifukwa Inu munawaitana iwo, ndipo mwinamwake iwo anali akungokonzekera kuti azichoka popanda kukulandirani Inu. Uwu, uthenga unabwereranso. Kotero ife tikupemphera, Atate Akumwamba, kuti Inu mupereke gawo lalikulu la Mzimu Wanu pa aliyense amene munthuyo angakhale ali. Inu simunatchule dzina lawo, Inu munangoyankhula. Ndipo chotero, Atate, mwinamwake umo ndi momwe Inu mukufunira izo. Ndipo ife tikungopemphera, Atate, kuti chifuniro Chanu chiperekedwe kwa munthu uyu kapena anthu awa, aliwonse omwe iwo angakhale ali, kuti izo zikhale zikubwera ku kuyitana komaliza. Ine ndikupemphera, Atate, kuti izo siziri, koma, mmawa uno ngati iwo ati alandire Iwo ndi kukhulupirira ndi mtima wawo wonse, atatha kumva Uthenga monga Inu munayankhulira ndi kunena, ndiyeno mulole iwo awulandire Iwo ndi chikho chokwezedwa, kuti alandire Mzimu. Mulole iwo awuke ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, kuloza ku chikhululukiro cha machimo awo, ndi kudzazidwa mokoma ndi Mzimu Woyera, ndi kutsogozedwa mu moyo wa utumiki ndi chisangalalo. Ine ndikupereka izi kwa Inu tsopano, Atate, ndi osonkhanawa, mu Dzina la Yesu. Ameni.

258 Mauthenga amenewo nthawizina amayankhula kwa, winawake, ife sitimadziwa omwe iwo ali. Nthawizina iwo amanena omwe iwo ali, koma basi winawake muno yemwe mwinamwake anangoyamba kuti azichoka wopanda

Iwo. Ndipo pamene inu mutero, kumbukirani, umenewo ndi Mzimu Woyera ukuyankhula mu chinenero chimene umangotenga kudzoza kwina; yemweyo amene anayankhula izo, yemweyo kutanthauzira izo. Tsopano, kumbukirani zomwe ine ndangotsiriza kumene kuwerenga, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira." Mwaona, ndizo pakati pa okhulupirira. Ife sitimakhulupirira kuti anthu onse akuyenera kumachita zimenezo. Ife timakhulupirira kuti iwo umagwera mu mpingo pakati pa anthu. Nthawizina anthu amabwera kuno, asanamvepo konse za chinthu choterocho, ndipo Mzimu Woyera umagwera pa iwo ndi kudzapereka uthenga, ndi kuchiritsa anthu amene akhala pamenepo akufa ndi khansa, ndi mitundu yonse ya matenda ndi zinthu, kubwereranso kachiwiri. Ndi Mzimu Woyera pakati pa anthu Ake.

259 Kodi inu mumamukonda Iye? Ameni. Ine ndimamukonda Iye, nanenso. Ife tikuyembekeza kuti tikuwonani inu usikuuno. Ndipo tsopano M'bale Neville, ine nditembenuzira msonkhanowu kwa M'bale Neville, m'busa wathu. Chabwino.



62-0603 Uvangeri Wa M'nthawi Yotsiriza
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org